
# Chinyengo Chachikuru Chikhala Poyera

## MKANGANO WAUKURU WOTSIRIZA M'DZIKO'LI UDZAKHALA WA TSIKU'LI

- **M'kati mwa kuukirana ndi mikangano pakati pa mapfuko, amitundu ya anthu ali mkati kuyezedwa ndi muyeso wokhala m'dzanja la Iye amene saphophonya.**
- **Kumwamba kuposa chinthu china chiri chonse. Ngati ife titaupeza moyo wosatha ndiye kuti talandira zonse; ndipo tikataya uwu tataya zonse.**



- **Sabata liri chizindikilo cha mphamvu ya kulenga ndi kupulumutsa; lionetsera Mulungu kuti ali magwero a moyo ndi chidziwitso; limakumbutsa ulemelero wa pa chiyambi wa munthu, ndi kuchitira umboni za cholinga chofuna kutilenganso mwatsopano ife m'chifanizo chake.**
- **Munthu aliyense ali ndi ufulu wakusankha mwakufuna kwake za moyo wake wamtsogolo.**

## CHINTHU CHACHIWIRI KUKHAZIKITSIDWA NDI MULUNGU

***(ndi chisankho cha moyo wanu wonse)***

### *CHILENGEDWE CHINACHITIRIDWA UMBONI NDI ZA KUMWAMBA*

"Pamenepo Yehova anayankha Yobu m'kabvumvulu, nati, Unali kuti muja ndinayika maziko a dziko lapansi? Muja nyenyezi za m'mawa zinayimba limodzi mokondwera ndi ana onse a Mulungu anapfuula ndi chimwemwe?" Werengani Yobu 38:1, 4, 7.

Muja ulemelero wa Mulungu "unaphimba miyamba, ndi dziko lapansi linadzala ndi kumlemekeza" Hab. 3:3.

Yesu anadzifotokoza Iye mwini kuti ali Nthanda, Nyenyezi yonyezimira ya mbanda kucha pa Chibv. 22:16. Nyenyezi ndi dzina lina lomwe angelo amatchulidwa nalo (Chibv. 1:20). Choncho sikungakhale kulakwitsa kuganiza kuti mau akuti "ana onse a Mulungu" amatanthauza amoyo onse olengedwa okhalawo m'mayiko ena onse a m'mwamba. Monga sichingakhalenso chinthu chothandiza kuganizanso kuti ife amene tiri pa dziko lapansi timayang'anidwa mwachidwi ndi angelo, kudzanso miyamba yonse? Wolemba Masalmo akufotokoza kuti munthu anachepsedwa "pang'ono ndi angelo" Mas. 8:5. KJV.

Zinthu zonse zinalengedwa ndi Mwana wa Mulungu. "Pachiyambi panali Mau, ndipo Mau anali kwa Mulungu. .. Zonse zinalengedwa ndi Iye; ndipo kopanda Iye sikunalengedwa kanthu kali konse kolengedwa." Yoh. 1:1-3.

Pachiyambi Atate ndi Mwana anapumula pa tsiku lachisanu ndi chiwiri pambuyo pa ntchito Yao ya kulenga. Pamene "zinatha kupangidwa zakumwamba ndi dziko lapansi, ndi khamu lao lonse" (Gen. 2:1), Mlengi pamodzi ndi khamu la amoyo akumwamba anakondwera poziona zolengedwazo ziri zodzala ndi ulemelero. "Nyenyezi za m'mawa zinayimba limodzi mokondwera. Ndipo ana onse a Mulungu anapfuula ndi chimwemwe." Yobu 38:7.

Mulungu anapereka umboni wokwanira kuti mphamvu yake iribe malire. Iye amaligwiriziza dziko lapansi ndi liu la mphamvu yake. Anaupanga mdima ukhale choonetsera kuwala kwa nyenyezi za mu mlengalenga. Amazitchula zonse ndi mayina ao. Zakumwamba zimalalikira ulemelero wa Mulungu, ndipo thambo lionetsa ntchito ya manja ake," (Mas. 19:1), kuwatsimikizira anthu kuti dziko lapansi laling'ono'li liri koma kanthu kochepetsetsa poliyerekeza ndi chilengedwe chonse.

Sabata limawatsogolera maganizo athu ku chilengedwe, ndiponso kutilumikizanitsa ndi Mlengi. M'liu lakuimba la mbalame, kuimba kwa mitengo, liu la kuimba la nyanja tingathe kupitirira kumvera mau a Mlengi monga Iye analankhulira ndi Adamu m'kamphepo ka kayaziyazi ndi kozizira bwino ka usana m' Edeni. Ndipo ife tikamayiona mphamvu ndi ukuru wake m'chilengedwe timadzala ndi chimwemwe, pozindikira kuti Mau amene analenga zinthu zonsezi ndi Iye amaperekanso moyo kwa munthu. Iye amene analamulira kuti kuunika kuwale "kuturuka mu mdima, ndiye amene amawala m'mitima yathu kutipatsa kuunika kwa chidziwitso cha ulemelero wa Mulungu pa nkhope pa Yesu Khristu." 2 Akor. 4:6.

Ndi pa ganizo ili pomwe panachokera nyimbo yakuti,-

"Inu Yehova munandikondweretsa ndi kuchita kwanu, Ndidzapfuula mokondwera pa ntchito ya manja anu.

Ha! Ntchito zanu nzazikuru, Yehova, Zolingalira zanu nzozama ndithu." Mas. 92:4,5.

Tsiku la chisanu ndi chiwiri loyamba linali la chimwemwe ndi chisangalalo chachikuru chomwe sichinachitikepo chilengedwere dziko lapansi. 'Wotsogolera wa Zochitika' za tsiku'lo sanali wina koma Yesu amene mosajejema konse akufotokoza kuti Ali Mbuye wa tsiku la Sabata. Iye [Yesu] anati kwa iwo, "Sabata linayikidwa chifukwa cha munthu…Motero Mwana wa munthu ali mwini dzuwa la Sabata lomwe." Marko 2:27, 28).

Mosachita kufunsa, Yesu amakhuzidwa ndi Sabata ndipo mtundu wa anthu, womwe ndi cholengedwa chaulemelero kupambana zolengedwa zina zonse, ndi woyenera kulilandira Sabata'lo ndi Yesu monga mphatso ziwiri za mtengo wapatali, zomwe timalephera kuzimvetsetsa. Mphatso za ulemelero woposa zotero.

Munthu anali cholengedwa chotsiriza cha chilengedwe chonse cha Mulungu, ndipo anapangidwa kukhala m'modzi ndi Mulungu. Munthu ndi wokondedwa kwambiri ndi Mulungu, chifukwa anapangidwa m'chifanizo cha Mulunguyo. Pamene Adamu anapangidwa kuchokera m'dzanja la Mlengi , anali wa msinkhu wautali bwino ndi wa maonekedwe abwino okongola. Kutalika kwake kunali kupinda kawiri katalikidwe ka anthu a nthawi ino, wodzongomala bwino ndi wa thanzi lopanda chibvundi. Hava, sanali wamtali ngati Adamu, msinkhu wake unali wotalikirako pang'ono kudutsa mapewa a Adamu, wodzala ndi chilemekezo chonse, wa thupi lokhuthala bwino ndiponso wokongola kwambiri.

Ku mapeto kwa tsiku'lo, (atatha angelo anabvala miinjiro yonyezimirawo ndiponso khamu lonse la zakumwamba kuyimba nyimbo zao za matamando ndi chiyamiko), Wopereka Malamulo Wamkurukuruyo, analipatula mwapadera tsiku lachisanu ndi chiwiri kukhala loyera kwa muyaya, ndi cholinga chakuti mtundu wa anthu usakhale wotayika m'dziko limene anali atangolilenga kumene, koma kuti udzikhala wodalitsika mu utatu wa Umodzi wa Mulungu kuyambira pamenepo. Chifukwa Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera analinso ali pomwepo pa tsiku lachisanu ndi chiwiri loyamba'lo.

### *KUPATULIDWA KWA TSIKU LA CHISANU NDI CHIWIRI MWAPADERA*

Atatha kupumula pa tsiku lachisanu ndi chiwiri Mulungu ndipo analiyeretsa ili kapenanso kuti kulipatula kuti likhale lakupumulanso la munthu. Motsatira chitsanzo cha Mlengi, munthu anauzidwa kupumula pa tsiku loyeretsedwa'li, kuti pa nthawi yakupulako akamayang'ana pa miyamba ndi dziko lapansi, adzikumbukira za ntchito yayikuru ya chilengedwe; ndiponso kuti poona zitsimikizo za luntha ndi ukuru wa Mulungu komanso ubwino wake, mtima wamunthuyo udzikhala wodzala ndi chikondi ndiponso chilemekezo pa Mlengi wake.

M'Edeni, Mulungu anayika chikumbutso cha ntchito yake yakulenga, ndi mdalitso wake pa tsiku lachisanu ndi chiwiri. Ndipo Sabata'lo linapatsidwa kwa Adamu,

atate ndi woimira wa banja la mtundu wonse wa anthu. Kusunga Sabata ndi kulilemekeza kunayenera kukhala njira imodzi ya kuyamika ndi kuthokoza, ku mbali ya anthu onse omwe anali kudzakhala pa dziko lapansi, kuti Mulungu ndi Mlengi wao ndi woyenera kukhaladi Mfumu yao; ndi kuti anthu'wo anali ntchito ya manja ake ndi nzika za ulamuliro wake. Ichi n'chifukwa chake Sabata linayenera kumakumbukidwa kwatunthu monga linapatsidwira ku mtundu wonse wa anthu. Ilo sinaperekedwa kuti kutsogolo kuno lidzakhale longosungidwa ndi anthu owerengeka kapena kukhala la mpingo wakutikuti ayi.

Mulungu analiona Sabata kuti n'lofunika kwambiri kwa munthu, ndipo lidzatero ngakhale ku Paradiso. Iye anafuna kuti padzikhala tsiku limodzi la masiku asanu ndi awiri momwe munthu adzikhala ndi nthawi yosiya ntchito zake za moyo uno ndikukhala ndi nthawi yapadera yolingirira ndi kuganizira za ukuru ndi ubwino wa Mulunguyo. Analifunitsitsa Sabata kukhala chomkumbutsa kotheratu za Iye mwini, ndi kudzutsa mwa munthu chizindikiritso ndi chiyamiko chakuti zonse zimene iye ali nazo kuphatikiza kumva kukoma kwa moyo uno n'zochokera m'dzanja lakupatsa mosalekeza la Mlengi.

Mulungu analikhazikitsa Sabata kukhala cholondolera maganizo a anthu kukulingirirapo za zinthu zonse zomwe zinalengedwa. Ndipo chilengedwecho chilankhule m'malingaliro ao, kulalikira za Mulungu wa moyo, yemwe ndi Mlengi, ndi Wolamulira Wamkurukuru wa zonse.

Sabata linapatulidwa pa chiyambi. Monga lopatulikira munthu, linakhazikitsidwa pa nthawi imene "nyenyezi za m'mawa zinayimba limodzi mokondwera, ndi ana onse a Mulungu anapfuula ndi chimwemwe." Yobu 38:7. Munali mtendere wochuruka m'dziko lapansi; chifukwa dziko'lo linali pachiyanjano ndi kumwamba. "Ndipo anaziona Mulungu zonse zimene adazipanga, ndipo taonani zinali zabwino ndithu." Napumula Iye ali wokondwa ndi ntchito imene anayichita. Gen.1:31.

Popeza anapumula Iye pa Sabata, "Mulungu ndipo anadalitsa tsiku lachisanu ndi chiwiri, naliyeretsa limenelo," – nalipatulira ku mautumiki ake oyera. Iye analipatsa ilo kwa Adamu likhale tsiku lakupumula. Linakhalanso chikumbutso cha ntchito yakulengedwa kwa zonse komanso chizindikiritso cha mphamvu ndi chikondi chake. Bukhu Lopatulika likutsindika ichi pakunena, "Analenga zodabwitsa zake kuti zizikumbukika." "Pakuti chilengedwere dziko lapansi zioneka bwino" ndi kulalikira "Zosaoneka zake ndizo mphamvu yake yosatha ndi umulungu wake." Gen. 2:3; Mas. 111:4; Arom. 1:20.

Mulungu analipatula tsiku la chisanu ndi chiwiri. Nthawi yopatulidwa mwapadera ndi Mulungu mwiniyi, nilekanitsidwa ndi kukhala yochitiramo zachipembedzo komanso kumpembedzera Iye, iri chikhalireyoyeretsedwa lero lino monga momwe inapatulidwira ndi Mlengi pachiyambi.

Zinthu zonse zinalengedwa ndi Mwana wa Mulungu. "Pachiyambi panali Mau, ndipo Mau anali kwa Mulungu…Zonse zinalengedwa ndi Iye; ndipo kopanda Iye sikukanalengedwa kanthu kali konse kolengedwa." John1:1-3. Choncho popeza Sabata liri chikumbutso cha ntchito yakulenga, lirinso chizindikiritso cha chikondi ndi mphamvu ya Khristu.

Lopatulidwa ndi Mulungu, Sabata linaperekedwa kusungidwa monga pangano la muyaya. Pokhala chikumbukiro cha chilengedwe, linakhazikitsidwa kukhala lochokera m'badwo wina kufikira ku unzake mpaka chimaliziro cha dziko lapansi ndi cha dziko liri nkudza.

Sabata likanasungidwa monga zinafunikira, likanawatsogolera maganizo ndiponso chikondi za munthu kwa Mlengi yemwe akanakhala akupembedzedwa ndi kupatsidwa ulemu woyenera, sipakanakhala opembedza mafano, okana kuti kulibe Mulungu kapena oukira a mtundu wina ali wonse. Chifukwa kusunga Sabata ndi chizindikiritso chakuti munthu wakutero ali womvera Mulungu woona, "Iye amene analenga m'mwamba ndi mtunda ndi Nyanja ndi akasupe a madzi."

## SABATA: MPHATSO YA MPUMULO

Sabata ndi la kale ndithu. Asanapatsidwe Malamulo Khumi pa Sinai Mose anatchulapo za ili pena pake m.Bukhu Lopatulika. "Ndipo ananena nao, Ichi ndi [chija] chomwe Yehova analankhula, Mawa ndiko (ndilo) kupuma, Sabata lopatulika la Yehova." Eksodo 16:23.

Ngakhale Sabata linaphatikizidwa ndi malamulo omwe anaperekedwa pa Sinai, omwenso ali a muyaya ndiye kuti ilonso silinali latsopano konse, linadziwika kukhala tsiku lakupumula kuyambira pa chilengedwe. Ana a Israyeli anazindikira za tsiku'li kale ndithu asanafike ku Sinai. M'njira popita ku Sinai'ko anasunga Sabata. Ena a iwo akaliipsya ili, Mulungu amawadzudzula, ponena nao, "Mukana kusunga zouza [zonena] zanga ndi malamulo anga kufikira liti?" Eksodo 16:28.

Sabata silinalengedwere Israyeli okha , koma mtundu wonse wa anthu. Linaperekedwa kwa munthu m'Edeni, ndipo monga ali Malamulo onse Khumi ndi lamuyaya losati nkusinthidwa mwachisawawa. Ponena za umuyaya wa Malamulo Khumiwo omwe lamulo lachinayi lao liri la Sabata'lo, Khristu anati, "Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kake kamodzi sikadzachokera kuchilamulo." Monga dziko lapansi ndi kumwamba zidzapitirira kukhalako chomwechonso lidzakhala Sabata kupitirira kukhala chizindikiritso cha mphamvu yakulenga ya Mlengi. Ndipo pamene Edeni adzabwezeredwanso pa dziko lapansi, tsiku la kupumula la Mulungu'li lidzalemekezedwabe ndi onse okhala pansi pa thambo. "Ndipo kudzakhala kuti kuyambira pa mwezi wokhala kufikira ku unzake, ndi kuyambira pa Sabata lina kufikira ku linzake, anthu onse adzafika kudzapembedza pamaso pa Ine, ati Yehova." Mat. 5:18; Yes. 66:23.

Chilengedwe chiyenera kumagwira ntchito zake ngakhale m'maora a tsiku lopatulika'li. Mulungunso samasiya kugwira ntchito yake mphindi ndi imodzi yomwe, pa tsiku'li, chifukwa atangotero munthu angathe kukomoka ndi kufa. Choncho munthu nayenso ali ndi ntchito yomwe ayenera kuichita pa tsiku'li. Zofunikira za moyo ziyenera kukwaniritsidwa, odwala kucherezedwa ndi kusamalidwa, ndi kupatsa kwa obvutika zosowa zao. Sadzayesedwa wosalakwa iye amene amalephera kuthandiza obvutika ati chifukwa chakuti ndi la Sabata. Tsiku lakupuma la Mulungu linalengedwa chifukwa cha munthu, kotero ntchito za chifundo zimagwirizana kotheratu ndi cholinga cha tsiku'li. Mulungu samafuna kuona chilengedwe chake chikumva kuwawa komwe kukanatha kupepukitsidwa pa tsiku la Sabata monga zikanachitikira tsiku lina liri lonse.

Ntchito imene Mulungu amayichita pa tsiku la Sabata imakhala yayikuru kuposa yomwe amayichita m'masiku a ntchito. Anthu ake amasiya zonse zodzisamalira okha nkumampembedza ndi kulingirira mwakuya za Iye. Amasiya chisamaliro chao chonse m'manja mwake napempha zifundo, chitchinjirizo ndi chisomo zake mowirikiza kuposa m'masiku ogwira ntchito. Amafuna chisamaliro chake mwapadera. Amafunitsitsa madalitso ake ochurukitsitsa. Ndipo Mulunguyo samayembekezera kuti Sabata lithe kuti ayankhe zifunsiro zao zonsezo. Nchito ya kumwamba simayima, chotero anthu nawonso asamapumule kuchita chinthu chiri chonse chabwino. Sabata Sinaikidwa kukhala lochitiramo zinthu zosayenera. Lamulo la Sabata'li limaletsa kuchita ntchito iri yonse ya za dziko pa tsiku la Ambuye'li; ntchito iri yonse yongokondweretsa umunthu isachitidwe; ntchito ziri zonse za dziko ndi zongodzisangalatsa kapena zodzifunira phindu la kuthupi zisachitike pa tsiku'li; ndipo monga Mulungu anatsiriza ntchito yake yakulenga, napumula pa tsiku la Sabata ndi kulidalitsa ili, chomwecho munthu asiye ntchito za moyo wake wa tsiku ndi tsiku, ndi kuwapatulira maora opatulika'wa kukupumula kopatsa thanzi labwino, kukupembedza ndiponso ku ntchito zina zonse zopatulika. Ntchito yakuchiritsa imene Khristu anayichita pa tsiku la Sabata inali yogwirizana ndi zofuna zenizeni za lamulo'li. Inalilemekeza Sabata.

Za mpumulo'wu, Mulungu anapereka chitsanzo Iye mwini: "Chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamaliza zakumwamba ndi zapansi, ndi Nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chake Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika." (Eks. 20: 8-11). Mpfundo iyi imakhala yomveka ndi yofunikira pa iwo amene amamvetsetsa za masiku akulenga kuti analidi masiku enieni. Ndikuti masiku oyambirira asanu ndi limodzi a pa mulungu uli wonse anapatsidwa kwa munthu kugwira ntchito zake zonse, chifukwa Mulungunso anagwiritsa nthawi yomweyo ya mulungu woyamba mu ntchito yake yakulenga. Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri munthu asagwire ntchito iri yonse pokumbukira mpumulo wa Mlengi.

Pachiyambi penipeni Atate ndi Mwana anapumula pa la Sabata atatha ntchito yao yakulenga. Pamene, "zinatha kupangidwa zakumwamba ndi dziko lapansi, ndi khamu lao lonse." (Gen. 2:1). Kufikira lero lino Mulungu amapumula ku ntchito yake ya kulenga, koma likudza tsiku pamene mapazi a osalungama sadzathanso kudetsa dziko lapansi latsopano. Moto udzatsika kuchokera kumwamba kwa Mulungu ndi kuwanyeketsa iwo, udzawaononga iwo kuyambira muzu mpaka nthambi. Satana ndiye muzu, ndipo ana ake ndiwo nthambi. Moto womwewo udzawaononge osalungama, udzayeretsa dziko lapansi. Pa nthawi imeneyo Mulungu, adzachita "zonse zikhale zatsopano." (Chibv. 21:5), zidzakhala nthawi "zakukonzanso zinthu zonse, zimene Mulungu analankhula za izo m'kamwa mwa aneneri ake oyera chiyambire." (Mac. 3:21), Sabata la chilengedwe, tsiku limenenso Yesu anapumula m'manda a Yosefe, lidzakhalabe lakupumula ndi la kukondwerera momwemo. Kumwamba ndi dziko latsopano zidzalumikizana kutamanda Mulungu, "kuyambira la Sabata lina kufikira kulinzake" (Yes. 66:23) pomwe amitundu onse opulumutsidwa adzawerame pansi kulemekeza Mulungu ndi Mwanawankhosa. Nthawi yomwenso "Ofatsa adzalandira dziko lapansi." (Mat. 5:5).

Yesu akuitanira moyo uli wonse kuti, "Senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine; chifukwa ndiri wofatsa ndi wodzichepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu." (Mat. 11:29).

Mphamvu yoyera ya uzimu imakhala chikhalire m'mawa uli wonse ndi madzulo ali onse. Imachotsa mwa munthu ali yense machitidwe onse akudzikuza komwe kuli magwero otsogolera ku mtundu uli wonse wa uchimo.

Mulungu anakonza kuti Sabata likhale chotsogolera maganizo a anthu kulingalira mwakuya za ntchito zomwe Iye anazichita. Chilengedwe chidzilankhula m'malingaliro ao, kulalikira kuti kuli Mulungu wa moyo, Mlengi ndi Mfumu ya onse. "Zakumwamba zimalalikira ulemelero wa Mulungu, ndipo thambo lionetsa ntchito za manja ake. Usana ndi usana uchurukitsa mau, ndipo usiku ndi usiku uonetsa nzeru." Mas. 19:1, 2. Kukongola komwe kwalikutira dziko lapansi kuli chisonyezo cha chikondi cha Mulungu. Timakuona uku pa mapiri anakhalawo kale lomwe, m'mitengo yayitali, mu mphukira za mitengo ndi m'maluwa owala. Zonsezi zimalalikira za Mulungu kwa ife. Sabata, limatilozera kwa muyaya kwa Iye amene analenga zonsezi, ndipo limawalimbikitsa anthu kuphunzira zambiri kuchokera ku bukhu lopambana la chilengedwe momwe mumapezeka luntha, mphamvu ndi chikondi cha Mlengi.

Lamulo lachinayi'li liri chikatikati cha malamulo oyambirira atatu omwe akukhuzidwa ndi momwe tingamampembedzere Mulungu ndiponso ubale wathu ndi Iye, ndi malamulo asanu ndi limodzi omwe akukhuzana ndi ubale wa munthu ndi munthu mnzake ndiponso udindo wathu pa anthu anzathu. Ulamuliro wa Mulungu ndi "chisindikizo" chake zikupezeka mu lamulo lachinayi'li, kotero kuti, ndi themberero la lalikuru ndi la muyaya ngati ife timanyalanyaza kapena kukana kusunga ndi kulilemekeza tsiku lachisanu ndi chiwiri.

Lamulo lachinayi'li limati: "Uzikumbukira tsiku la Sabata likhale lopatulika. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumariza ntchito zako zonse; koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako; usagwire ntchito iri yonse, kapena iwe wekha, kapena mwana wako wamwamuna, kapena mwana wako wamkazi, kapena wantchito wako wamwamuna, kapena wantchito wako wamkazi, kapena nyama zako, kapena mlendo amene ali m'mudzi mwako; chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamariza zakumwamba ndi za pa dziko lapansi, ndi Nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chake Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika." Eksodo 20:8-11.

Kupumula osalingalira nako chiri chonse pa tsiku la Sabata kapena tsiku lina liri lonse sindiko kusunga Sabata koona, ndipo zisamakhale choncho mpaka kalekale. Kusunga Sabata la Yehova kuyenera kuchitika kuyambira mu mtima, m'moyo wa mkati ndi mwa chikhulupiriro mwa Khristu. Ndi munthu yekhayo amene ali ndi khalidwe la kudzichepetsa ndi kudzikhuthula la Khristu, napumula mwa Iye, yemwe angathe kulowa mu mpumulo kapena kusunga Sabata la Ambuye moyenera. Ndipo yense amene amapeza mpumulo mwa Khristu alowa mu mpumulo'wo mwa chikhulupiriro kudzera mu nsembe ya Yesuyo yakutsuka ndi kutetezera machimo; iye amapeza mpumulo m'ziphunzitso za Khristuyo ndiponso m'chitsanzo chake. Woteroyo amakondwera pomtsatira Khristuyo m'zinthu zonse. Yesu'tu sanasunge tsiku la Sabata lina la pa mulungu koma lija lomwe Iye analikhazikitsa lomwenso ndi la Sabata la Atate amenenso anapumula, atatha kulenga zinthu zonse m'masiku asanu ndi limodzi. Sabata la Ambuye likasungidwa mwa chikhulupiriro mwa Khristu, limakhala chikumbutso chopindulitsa cha chilengedwe chomwe chinachitika pa chiyambi, komanso cha kulengedwa mwatsopano kwa mitima yathu komwe kunadza ndi mphamvu ndi chikondi zizikuru. Lirinso chikole cha moyo wosatha mu ufumu wa ulemelero; chifukwa Mzimu Woyera amakhala atalemba Sabata'lo m'mitima mwathu, ndipo mwa Mzimu yemweyo timasindikizidwa chizindikilo kufikira tsiku lachipulumutso. Aef. 4:30.

"Kodi iwe sunadziwe? Kodi sunamve? Mulungu wachikhalire, Yehova, Mlengi wa malekezero a dziko lapansi, salefuka konse, salema; ... Iye alimbitsa olefuka, naonjezera mphamvu iye amene alibe mphamvu." "Usaope, pakuti Ine ndiri pamodzi ndi iwe; usaopsyedwe, pakuti Ine ndine Mulungu wako ndidzakulimbikitsa; inde, ndidzakuthangata; inde, ndidzakuchirikiza ndi dzanja langa lamanja la chilungamo." "Yang'anani kwa Ine mupulumutsidwe, inu malekezero onse a dziko; pakuti Ine ndine Mulungu, palibe wina." "Mudzipatulanso masabata anga, ndipo adzakhala chizindikilo pakati pa Ine ndi inu, kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu." Yes. 40:28-29; 41:10; 45:22; Ezek. 20:20.

## *MLUNGU WENIWENI WA MASIKU ASANU NDI AWIRI*

Monga Sabata, mlungu unalengedwa pachiyambi pa chilengedwe, ndipo unasungidwa mu mbiri yonse ya Bukhu Lopatulika kufikira lero. Mulungu mwini wake anautenga mlungu woyambirira kulengedwa kukhala chitsanzo cha milungu yonse yobwera pambuyo pa uwu mpaka nthawi ya chimaliziro. Monga uli mlungu uli wonse ndi masiku enieni asanu ndi awiri pano, ndimo unali mlungu wa pachiyambiwo.

Mu lamulo lomwe analipereka pa Sinai, Mulungu analankhulamo zokhuza mlungu, ndiponso zifukwa zimene anaukhazikitsira. Iye anati, "Uzikumbukira tsiku la Sabata likhale lopatulika," nafotokozanso zinthu zomwe zinayera kuchitika m'masiku asanu ndi limodzi, ndi zomwe sizinayenera kuchitika pa tsiku lachisanu ndi chiwiri, ndipo anapereka chitsanzo cha Iye mwini za masungidwe a mlungu'wo: "Chifukwa kwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamariza zakumwamba ndi za dziko lapansi, ndi Nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chake Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika." (Eks. 20:8-11). Chifukwa ichi chimamveka bwino kwambiri ndi kukhala chofunika ngati titamvetsetsa za masiku a chilengedwe kuti analidi masiku enieni osati chiphiphiritso. Masiku asanu ndi limodzi a pa mlungu anapatsidwa kwa munthu kuti adzigwiramo ntchito zake chifukwa Mulungu nayenso anagwiramo ntchito yake ya kulenga pa mlungu woyambawo. Pa tsiku la chisanu ndi chiwiri munthu anauzidwa kuti asagwire ntchito kuti pakutero adzikumbukira mpumulo wa Mlengi.

Choncho chiphunzitso chakuti chilengedwe chinatenga zaka zikwizikwi chikuchitidwa, chikutsutsana kotheratu ndi choonadi chomwe lakhazikikapo lamulo lachinayi. Tikatenga chiphunzitso cholakwikacho, zikumveka ngati kuti Mlengi analamulira anthu kutenga tsiku lenileni la pa mlungu kuimira nthawi yayitali, ya zaka zochuruka. Uku nkutsutsana ndi momwe Mlengiyo akuchitira nazo zinthu zomwe Iye anazilenga. Chiphunzitsochi chimasokoneza choonadi chenicheni cha chindunji ndi chomveka bwino cha mlungu wa pa chilengedwe. Icho chiri machenjerero okhala ndi upandu waukuru mkati mwake; cholinga chake chenicheni chimabisidwa kotero kuti chikumatha kuphunzitsidwa ngati choonadi ngakhale zisali choncho ndiponso ambiri a iwo ochiphunzitsa amati amakhulupirira Bukhu Lopatulika, Bukhu Lopatulika lokha.

"Zakumwamba zinalengedwa ndi mau a Yehova; ndipo mpweya wa m'kamwa mwake khamu lao lonse." "Pakuti ananena, ndipo chinachitidwa; analamulira, ndipo chinakhazikika." (Mas. 33:6, 9). Bukhu Lopatulika silikufotokoza za zaka zambirimbiri momwe dziko lapansi linanka likusinthika kuchokera m'machitidwe osiyanasiyana (evolution). Zolembera Zoyera'zi zikufotokoza za tsiku liri lonse kuti linatsatana ndi la chilengedwe linzake lopangidwa ndi madzulo ndiponso m'mawa, monga momwe ali masiku ena onse omwe anatsatira. Ndipo kumapeto



## *USIKU NDI USANA*

a tsiku liri lonse kukuperekedwa zotsatira za ntchito iriyonse imene Mlengi anayichita. Kufotokoza komveka bwino kwa zomwe zinachitika pa mlungu wa pachilengedwe kukuperekedwa. "Imeneyo ndiyo mibadwo yao ya zakumwamba ndi dziko lapansi, pamene zinalengedwa." (Gen. 2:4). Kutchulidwa kwa 'mibadwo,' sizikutanthauza kuti tsiku la mlungu wa chilengedwe linali nthawi ya zaka zambiri koma tsiku lenileni. Tsiku liri lonse linatchedwa m'badwo, chifukwa m'limene'lo Mulungu amalenga, kapena kupanga, zinthu za tsopano mwa mitundu yao yochuruka m'ntchito anayichitayo.

## CHITSIMIKIZO CHA MASIKU ASANU NDI AWIRI M'CHILENGEDWE

Sayansi yatsopano ya "Chronobiology" yachita mbali yayikuru kwambiri pakutsimikizira za momwe zinthu zinakhalira "pachiyambi pachilengedwe" ndi kulengedwa kwa masiku asanu ndi awiri a pa mlungu monga zaturukiridwira m'tidziwalo tating'ono ta thupi la munthu (cells) komanso mu tiziwalo ta mtundu womwewo ta za moyo zina.

Mwachidule, Chronobiology ndi kufufuza za momwe zinthu za moyo zimachitira nayo nthawi.

Chronobiology si phunziro laling'ononso m'Sayansi. Za phunziro'li a Perry ndi a Bawson akuti "... pano likuphunziridwa m'sukulu zikuruzikuru ndi zotchuka za ukachenjede komanso za za umoyo m'dziko lonse lapansi. Pali akatswiri ochuruka a phunziro'li omwe akugwira ntchito ku National Aeronautics and Space Administration [Bungwe Loyendetsa za Zamlengalenga] (NASA), komanso ku National Institute of Health [Bungwe la za Umoyo) ndiponso mabungwe ena a zofufuzafufuza a boma. Phunziro'li likukulirakulira monga limodzi la ena onse a Sayansi odziwika bwino, ndipo likuthandiza kusintha za kamvetsedwe ka kulumikizana kwa moyo ndi kawerengedwe ka nthawi.

Chimodzi cha kawerengedwe ka nthawi pogwiritsa ntchito za moyo ndi chija chokhuza zamoyo ndi mlungu wa masiku asanu ndi awiri. Mu umodzi wa mitu ya m'bukhu lake wotchedwa "Kufunikira Kwa Nthawi, (The Importance of Time" Jeremy Campbell akufotokoza:

"Pofufuzafufuza za mayendedwe a nthawi, chronobiology ya makono

yaturukira choonadi chodabwitsa za mlungu wa masiku asanu ndi awiri. M'zaka khumi ndi zisanu zapitazo, asayansi ena amakhulupirira kuti mlungu, unali kuimira zaka zambiri zakukhala ndi kusinthika kwa moyo. Pano zatsimikizika kuti mlungu wa chilengedwewu sunali zaka koma masiku enieni ndipo kayendedwe ka masiku'wo kakupezekanso m'ziwalo za zinthu za moyo zazing'ono kuyambira zokhala ndi kachiwalo kamodzi (one-cell) mpaka mu tamoyo tochepetsetsa (bacteria) tosaoneka ndi maso." "Pakuti chilengedwere dziko lapansi zaoneka bwino zosaoneka zake ndizo mphamvu yake yosatha ndi umulungu wake; popeza zazindikirika ndi zinthu zolengedwa, kuti iwo adzakhale opanda mau akuwiringula." (Arom. 1:20).

Tikamvetsa bwino za chilengedwe chotizungulira ndi za moyo wathu wodabwitsa, tidzawakana onyoza Mulungu monga wolemba Masalmo wanena, "Wautsiru amati mumtima mwake, kulibe Mulungu." (Mas. 14:1).

### *TSIKU LACHISANU NDI CHIWIRI*

Ngakhale anthu anzeru zakuya chotani sangathe kumvetsetsa chinsinsi cha Mulungu. "Njira zake nzosalondereka." (Arom. 11:33).

Chilengedwe chonse chitachitika. "Ndipo zinatha kupangidwa zakumwamba ndi dziko lapansi, ndi khamu lao lonse." "Ndipo anaziona Mulungu zonse zimene adazipanga, ndipo taonani, zinali zabwino ndithu." Edeni anawala monga duwa m'dziko lapansi. Adamu ndi Hava anali ndi ufulu wonse wakudya za mtengo wamoyo.

Pamene maziko a dziko lapansi anayalidwa, ndipo nyenyezi za m'mawa zinayimba limodzi mokondwera ndi ana onse a Mulungu anapfuula ndi chimwemwe, ndi nthawi yomwenso Sabata linakhazikitsidwa. Choncho nkoyenera kuti mpumulo uwu ulandire chilemekezo chathu; sunakhazikitsidwa ndi chifuniro cha munthu ndi kumangika pa miyambbo ya umunthu; unayikidwa ndi Nkhalamba Yakale Lomwe ndi kuperekedwa mwa liu la muyaya lake.

Asanalengedwe munthu angelo anali alipo ngati mbali ya khamu la kumwamba.

Sabata linapatsidwa ku dziko lapansi ndi Mulungu, kuti munthu adzimkumbukira Iye kuti ali Mulungu woona ndi wamoyo.

Sabata linapatulidwa (kukhala loyera) pa chilengedwe. Mtendere unadzala dziko lonse; chifukwa linali m'chiyanjano chenicheni ndi kumwamba. "Ndipo anaziona Mulungu zonse zimene anazipanga, ndipo, taonani, zinali zabwino ndithu;" ndipo anapumula Iye ali wodzala ndi chimwemwe pa ntchito imene anayichita. Gen. 1:31.

Momwe amachokera m'dzanja la Mulungu, si Edeni yekha koma dziko lonse linali lokongola ndithu. Panalibe kabanga kalikonse ka uchimo, kapena mthunzi wa imfa, popeza izi zikanayipitsa chilengedwe chokomacho. Ulemelero wa Mulungu, "unaphimba miyamba, ndi dziko lapansi linadzala ndi kumlemekeza." Habakuku 3:3. Umo ndimo dziko lapansi linakhalira chizindikiritso cha ukuru wa Iye amene ali "wa ukoma mtima wochuruka ndi wachoonadi" (Eksodo 34:6); choyenera kuphunziramo nzeru anthu amene anapangidwa m'chifanizo chake.

Pa nthawi imene maziko a dziko lapansi amayalidwa, ndi nthawi yomwenso linakhazikitsidwa Sabata. "Muja nyenyezi za m'mawa zinayimba limodzi mokondwera, ndi ana onse a Mulungu anapfuula ndi chimwemwe," Mulungu anaona kuti Sabata linali lofunika kwa munthu, komanso m'Paradiso. Popereka Sabata, Mulungu anaganizira za thanzi la uzimu komanso thanzi la thupi la munthu. Kukana kusunga Sabata, kungofanana ndi kukana madalitso.

"Mulungu ndiye chikondi" (Yohane 4:16). Chikhalidwe chake, chilamulo chake ziri chikondi. Ichi chakhala chiri; ndipo chidzapitirira kukhala chomwecho. "Iye amene ali wamtari wotukuridwa, amene akhala mwachikhalire" (Yesaya 57:15), amene "mayendedwe ake ndiwo a kale lomwe" (Habakuku 3:6, sasintha. Iye "alibe chisanduliko, kapena mthunzi wa chitembenukiro." (Yakobo 1:17).

Maonekedwe a mtundu uli wonse wa mphamvu yakulenga akuonetsera chikondi chosatha. Ndipo ukuru wa Mulungu uphatikiza mkati mwake mdalitso wochurukitsa kwa olengedwa ake onse.

### SABATA LIMALIMBIKITSANSO KUMVERA MULUNGU

Pokhala Iye Mlengi chinthu chirichonse chiyenera kudzichepetsa pamaso pa Mulungu.

"Ngati musunga malamulo anga m'dzakhala m'chikondi changa; monga Ine ndasunga malamulo a Atate wanga, ndipo ndikhala m'chikondi chake." Yohane 15:10.

Mulungu osati Adamu kapena Hava ndiye ali mutu weniweni wa masiku asanu ndi limodzi a chilengedwe. M'mutu woyamba wa Genesis wokha mukupezeka mau ofotokoza za Mulungu makumi atatu monga, "Mulungu analenga;" "Mulungu anati;" "Mulungu anaona:" "Mulungu anayitana;" ndiponso "Mulungu anadalitsa." Kubwerezabwereza mau koteroku, kukutitsimikizira kotheratu kuti Mulungu ndiye analenga chinthu chiri chonse m'masiku asanu ndi limodzi oyambirira aja. Palibe chimene anapangapo munthu.

Ganizo'li likungofokozanso za choonadi cha tsiku la chisanu ndi chiwiri monganso lachitira za masiku asanu ndi limodzi. Mulungu ndiye analenga tsiku lachisanu ndi chiwiri monganso anachitira ndi masiku asanu ndi limodzi.

"Tsiku lachisanu ndi chiwiri **Mulungu** anamariza ntchito **Yake** yonse **Iye** anayipanga; ndipo **Iye** anapuma tsiku lachisanu ndi chiwiri ku ntchito **Yake** yonse **Iye** anayichita. **Mulungu** ndipo anadalitsa tsiku lachisanu ndi chiwiri, naliyeretsa limenelo, chifukwa m'limenelo **Iye** anapuma ku ntchito **Yake** yonse imene Mulungu anayilenga ndi kupanga." (Gen. 2:2, 3).

Tsiku la Sabata la pa mlungu uli wonse la m'lamulo lachinayi limatsogolera malingaliro athu ku Chilengedwe ndi mautumiki omwe mtundu wa anthu uyenera kuwachita pofuna kuonetsa kumlekeza Mlengi kwao ndiponso monga olengedwa ake. Timampembedza Mulungu makamaka chifukwa ali Mlengi wathu: "Tiyeni, tipembedze tiwerame; tigwade pamaso pa Yehova amene anatilenga." (Mas. 95:6). Lamulo la Sabata limalimbikitsa udindo wathu wakupembedza Mulungu ndi kutitsogolera ife ku kapembedzedwe kolondora. Monga momwe chilengedwe chidzakhalabe chikhalire ife tidzakhalabe tikulikumbukira Sabata monga lopatulika lokumbukira chilengedwe: "Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kake kamodzi sikadzachokera kuchilamulo, kufikira zitachitidwa zonse." (Mat. 5:18). Mulungu sadzasintha chifuniro chake. Lamulo lake ndi la chikhalire. (Mas. 119:89, 152, 160).

Mosachita kufunsa konse, lamulo lachinayi limalumikizitsa malamulo atatu oyambirira ndi malamulo asanu ndi limodzi otsiriza. Kusunga Sabata sikumangothandiza kukhala ndi chikhulupiriro kokha mwa Mulungu, ndi kugonjera kuchifuniro chake kokha, koma limakhuzanso udindo wathu kwa munthu mnzathu ndi kwa nyama komanso kwa ife eni. Kumatithandizanso kulimbikitsa ndi kutchinjiriza miyoyo ndi thanzi lathu, miyoyo ndi thanzi la antchito athu komanso thanzi la nyama zimene zimatigwirira ntchito. Potipanga ife kukhala ndi nthawi yakulingilira, kupembedza komanso kukhala pachiyanjano m'mautumiki akupembedza, Sabata limatichotsera kudzikonda ndi kukhala moyo woyenera. Lamulo la chinayi ndi la dziko lonse lapansi, lopambana, lompangitsa munthu kulingirira za chimene likumphunzitsa, ndiponso lolimbikitsa kukweza ubwino wa munthu ndi kuletsa kuwachitira chosayenera anthu ena. Limalimbikitsanso kupereka ulemu ku ulamuliro ndi ukuru wa Mulungu ndi kugonjera choonadi. Limaletsa kusaweruzika kuli konse.

Mwa malamulo onse khumi, lamulo la Sabata ndi lokhalo lomwe limamtchura Mulungu kuti ndiye amapatsa malamulo'wo, udindo wake ndi malo komwe ulamuliro wake umachitikira. Sabata liri chikatikati cha Malamulo Khumi chifukwa ndi lofunikira kwambiri ponena za mphamvu ya Malamulo Khumi'wo ndiponso chomangirira pamodzi cha magome awiri amiyala pomwe palembedwa malamulo okhuza ubale wa Mulungu ndi munthu komanso wa munthu ndi munthu mnzake. Tikalitenga monga likufunikira likuoneka kuti likupatsa machitidwe omwe amalimbikitsa kuti chiyero chinke chikukulirakulira. Lamulo la Sabata ndi chimodzi cha ziphunzitso zofunikira ndi zopambana kwambiri m'Bukhu Lopatulika.

M'modzi wa alembi a Mpatuko (Protestants) a Richard Winter Hamilton, LL.D., D.D. m'zaka za m'ma 1800 akufotokoza kufunikira kwa Sabata la pa mlungu uliwonse motere:: "Sabata monga tikulionera liri gawo la malamulo khumi a Mulungu. Ilo silinayikidwa m'malamulo'wo kwachabe, koma kuti lipereke tanthauzo ndi cholinga chenicheni cha malamulo'wo. Chikhristu sichingakhale cha tanthauzo popanda ili. Ndi ili "inde,timakhazikitsa lamulo." Sabata siliri mbali ya malamulo a zinsembe ndi pang'onopang'ono pomwe. Si liri mthunzi wa chinthu china chiri chonse koma wa ilo leni. Silingathe kusinthanitsidwa ndi china chiri chonse. Sabata ndi Sabata basi, ndipo silingathe kukhala chinthu china chiri chonse koma Sabata. Sabata ndi limodzi la malamulo ozindikiritsa tchimo ndipo ganizo lakuti mpumulo'wu unali m'thunzi wa zinthu zinali nkudza ndipo linathetsedwa ndi Yesu Khristu m'Akolose 2:14-17, si zoona. Poyang'ana zaka makumi anayi zinali nkudza m'tsogolo pomwe kachisi ku Yerusalemu anaphwasulidwa, m'chaka cha 70 A.D., Yesu anakweza chiyero cha Sabata pa Mateyu 24:20. Pofotokoza za m'dziko la muyaya lomwe liri nkudza ndi Sabata, Yesaya pa Yesaya 66:22, 23 ananenera kuti la Sabata la pa mlungu lidzapitirira kusungidwa ndi kukhalabe lakupembedza pamaso pa Mulungu.

Tiyeni timvere chimaliziro cha zonse tsono: "Opa Mulungu, musunge malamulo ake; pakuti (chinthu) choyenera (kuchita ) anthu onse ndi ichi.

Pakuti Mulungu adzanena mlandu wa zochita zonse, ndi zobisika zonse, ngakhale (zikhale) zabwino ngakhale (zikhale) zoipa." Mlaliki 12:13, 14.

### MALAMULO ALI CHIKHALIDWE CHENICHENI CHA MULUNGU

Mulungu ndiye mzimu (Yohane 4:24) Chilamulo chake chiri cha Uzimu (aroma 7:14).

Mulungu ndiye chikondi (1 Yohane 4:8) Chilamulo chake chiri chikondi (Mateyu 22:37-40).

Mulungu ndiye choonadi (Yohane 14:6) Chilamulo chake ndicho choonadi

(Masalmo 119:142).

Mulungu ndiye chilungamo 1 Akor. 1.30) Malamulo ake onse ndi olungama (Masalmo 119:172).

Mulungu ndi Woyera (Yesaya 6:3) Chilamulo chake ndi choyera (Aroma 7:12).

Mulungu ndi wabwino (Luka 18:19) Chilamulo chake ndi chabwino (Aroma 7:12).

Mulungu ali wangwiro (Mateyu 5:48) Chilamulo chake chiri changwiro (Masalmo 19:7).

Mulungu ndi wamuyaya (Yakobo 1:17) Malamulo ake achirikizika ku nthawi za nthawi (Masalmo 11:7, 8).

Mulungu ndi wolungama (Deuteronomo 32:4) Chilangizo chake ndi cholungama (Aroma 7:12).

Mulungu wopanda banga la uchimo (1 Yohane 3:3) Malamulo ake ndi opanda banga la uchimo (Masalmo 19:8)

Mulungu sasintha (Yakobo 1:17) Chilamulo chake sichisintha (Mateyu 5:18).

Mulungu ndi kuunika (1 Yohane 1:5) Malamulo ake ali kuunika (Miyambo 6:23)

Mulungu ali chilungamo (Aroma 1:17) Malamulo ake ali chilungamo (Masalmo 119:172)

Mulungu ali Wokhulupirika (1 Akor. 10:13) Chilamulo chake ndi chokhulupirika (Mas. 119:86).

Mulungu ndiye Nzeru (Yobu 12:12, 13) Malamulo ake amapatsa nzeru (Masalmo 111:10; 119:98)

Mulungu ndi Wamkuru (Yobu 36:26) Chilamulo chake ndi chotakata (Hosea 8:12

Mulungu ali Mtendere (2 Akor. 13:11) Okonda chilamulo chake apeza mtendere (Masalmo 119:165).

## MALAMULO A MULUNGU ALI CHITCHINJIRIZO CHA MACHIMO

[Malamulo ake] achirikizika ku nthawi za nthawi, achitika m'choonadi ndi chilunjiko." Mas. 111:8.

Ha! Ndikondadi chilamulo chanu, ndilingiliramo ine tsiku lonse.

Malamulo anu andipatsa nzeru yoposa adani anga, pakuti akhala nane chikhalire.

Ndiri nayo nzeru yakuposa aphunzitsi anga onse, pakuti ndilingalira mboni zanu.

Ndizindikira koposa okalamba popeza ndinasunga malangizo anu.

Ndinaletsa mapazi anga njira iri yonse yoipa, kuti ndisamalire mau anu.

Sindinapatukana nao maweruzo anu, pakuti Inu munandiphunzitsa.

Mau anu azunadi powalawa Ine! koposa uchi m'kamwa mwanga.

Malangizo anu andizindikiritsa, chifukwa chake ndidana nao mayendedwe onse achinyengo.

Mau anu ndiwo nyali ya kumapazi anga, ndi kuunika kwa panjira panga.

Ndinalumbira, ndipo ndinatsimikiza mtima, kuti ndidzasamalira maweruzo anu olungama.

Ndizunzika kwambiri: ndipatseni moyo, Yehova, monga mwa mau anu.

Landirani, Yehova, zopereka zaufulu za pakamwa panga, ndipo ndiphunzitseni maweruzo anu.

Moyo wanga ukhala m'dzanja langa chikhalire, koma sindiiwala chilamulo chanu.

Oipa ananditchera msampha, koma sindinasokera m'malangizo anu.

Ndinalandira mboni zanu zikhale cholandira chosatha, pakuti ndizo zokondweretsa mtima wanga.

Ndinalingitsa mtima wanga uchite malemba anu, kosatha kufikira chimariziro.

Ndidana nao a mitima iwiri, koma ndikonda chilamulo chanu

Inu ndinu pobisala panga, ndi chikopa changa, ndiyembekezera mau anu. Mas. 119:97-114.

"Si kuposa kwa chilamulo, koma ukulu wa Iye Wakuchipereka, kuti chikhale muyeso wakumvera. Anthu ena angathe kunyozera malamulo ang'ono awa ndi ooneka ofooka'wa kuwatenga ngati opanda pake. Koma cholinga cha malamulo'wa ndicho kukuyesa kumvera kapena kusamvera, monga momwe zinachitikira m'Edeni pansi pa mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa. Cholinga chenicheni ndi chakuti: Kodi Mulungu ngoyenera kumveredwa pa zonse akuzilamulira? Kodi Iye ndi wopereka malamulo woyerayo? Kodi zolengedwa zake ndi zoyenera kumvera ndi kuchita chifuniro chake? Andrew Bonar, kufotokoza zokhuza malamulo omwe ali m' Levitiko, zokopedwa kuchokera m'zolembera za a J. Bridges m'bukhu lao The Pursuit of Holiness (Kuchifunitsitsa Chiyero), p. 23.

Munthu ali yense wakuswa limodzi la malamulo khumi mwadara, nkumasunga otsala'wo, asadzinamize kuti akusunga malamulo'wo mu mzimu ndi m'choonadi. "Pakuti amene ali yense angasunge malamulo onse, koma akakhumudwa (akalakwa) pa limodzi iyeyu wachimwira onse." (Yakobo 2:10).

Sikukula kwa tchimo kumalipanga tchimo kukhala tchimo, koma kuchita motsutsana ndi chifuniro cha Mulungu kuli konse, kungachepe; pakuti kutero kumaonetsa kuti pali kulumikizana pakati pa munthu ndi tchimo. Mtima umagawika m'zochita zake. Pamakhala kumkana Mulungu, komanso kutsutsana ndi malamulo a ulamuliro Wake.

Anthu akanapatsidwa ufulu kusiya kuchita chifuniro cha Mulungu ndi kukhazikitsa malamulo aoao aliyense payekhapayekha, pakanakhala malamulo osiyanasiyana pakayendetsedwe kazinthu mogwirizana ndi maganizo a munthu aliyense payekha ndipo ulamuliro pa zinthu zonse ukanachotsedwa m'manja mwa Mulungu. Chifuniro cha munthu chikanakwezedwa, ndipo chifuniro cha ukuru ndi chiyero cha Mulungu – cholinga cha chikondi chake pa zolengedwa zake – chikanakhala chonyozedwa ndi chosalemekezedwa.

Nthawi iri yonse pamene anthu amasankha kuchita zinthu m'njira za umunthu wao, amakhala pa choopsya chakulimbana ndi Mulungu. Iwo sangakhale ndi malo mu ufumu wakumwamba, chifukwa amakhala akutsutsana ndi malangizo owatsogolera kumwambako. Ponyalanyaza chifuniro cha Mulungu, amadziika iwo eni ku mbali ya Satana, yemwe ndi mdani wa Mulungu ndi munthu. Osati ndi liu lakutilakuti lokha, kapena ndi mau ena nkusiyako ena ayi, koma ndi mau onse oturuka pakamwa pa Mulungu, munthu adzakhala nao ndi moyo. Sitinganyalanyaze liu limodzi la Mulungu, ngakhale lioneke lonyozeka chotani kwa ife, nkukhala ndi moyo. Liri lonse la mau ndi malamulo a Mulungu linaperekedwa ku ubwino ndi chisangalalo cha munthu, kuyambira m'moyo uno kufikira m'moyo ulinkudza.

Kunenanso mobwereza, liri lonse la mau ndi malamulo a Mulungu linaperekedwa ku ubwino ndi chisangalalo cha munthu, kuyambira m'moyo uno kufikira m'moyo ulinkudza. Pakumvera ndi kuchita malamulo a Mulungu, munthu amazungulidwa monga umachitira mpanda ndi kutchinjirizidwa kuchokera ku tchimo. Choncho munthu ali yense amene amaphwasula tchinjirizo lomangidwa ndi Mulungu ili mu njira imodzi kapena inzake amaononga mphamvu yakumtchinjiriza mwini yekha; chifukwa pakutero amatsegula njira yakuti mdani alowe kwa iye kuti amuphe ndi kumuononga.

Chipembedzo chongoyang'anira pa lamulo nchosakwanira kuuyanjanitsa moyo ndi Mulungu. Koma chikhulupiriro choona ndi chija "chakuchititsa mwa chikondi" (Agal. 5:6) ndi choyeretsa mtima. Icho chiri ngati chotupitsa chomwe chimalisintha khalidwe. Yesu anapitiriza kuwaonetsera anthu omwe amamvetsera tanthauzo lakusunga malamulo a Mulungu – kuti ndiko kukhala ndi khalidwe ngati la Khristu mwa iwo eni.

Posamvera ndi kunyalanyaza chifuniro cha Mulungu m'nthawi ya kaleyo, makolo athu oyambirirawo anatsegula namondwe wa mabvuto pa dziko lapansi. Ndipo ali yense amene akutsatira chitsanzo chao adzakolora zotsatira ngati zimene makolo athu'wo anakolora. Chikondi cha Mulungu chionekera mu liri lonse la malamulo ake, choncho ali yense amene amasiya kusunga malamulo'wo akudziitanira pa iye mwini moyo wakusakondwa ndi chionongeko.

Mtendere wa munthu uyenera kutchinjirizidwa ndi lamulo la Mulungu nthawi zonse. Ndi pakumvera, kusunga ndi kuchita malamulo a Mulungu pomwe munthu angapeze mtendere weniweni. Malamulo ndiwo mpanda umene Mulungu wauika mozungulira kutchinjiriza munda wake wa mpesa. Onse amene amasunga malamulo amatchinjirizidwa ku tchimo. Mu kulakwa Adamu anadzikhalira lamulo kwa mwini



yekha. Ndipo pakusamvera anakhala 'pansi pa lamulo.' Umu ndimo chiyambi chakudzikuza, ndi kudzikonda, chinalowera m'moyo wa munthu. Chifuniro cha munthu ndi chifuniro cha Mulungu sizinathekenso kulumikizana. Adamu analumikizana ndi ankhondo oukira, ndipo mtima wakudzikuza unamlowa.

## *MALAMULO A MULUNGU M'CHIPANGANO CHATSOPANO*

**1**

Mateyu 4:10. "Ambuye Mulungu wako udzamgwadira, ndipo Iye yekha udzamlambira."

**2**

1 Yohane 5:21."Tiana, dzisungireni nokha kupewa mafano."

**3**

1 Timoteo 6:1. "Kuti dzina la Mulungu ndi chiphunzitso zisachitidwe mwano."

**4**

Ahebri 4:4, 9."Pakuti wanena pena za tsiku lachisanu ndi chiwiri, natero, Ndipo Mulungu anapumula tsiku lachisanu ndi chiwiri, kuleka ntchito zake zonse. Momwemo utsalira mpumulo wa Sabata wa kwa anthu a Mulungu."

**5**

Aefeso 6:2. "Lemekeza Atate wako ndi amako."

**6**

Aroma 13:9."Usaphe"

**7**

Mateyu 19:18. "Usachite chigololo"

**8**

Aroma 13:9."Usabe"

**9**

Aroma 13:9."Usamnamizire mnzako"

**10**

Aroma 13:9."Usasirire"

## "NGATI MUKONDA INE SUNGANI MALAMULO ANGA"

Pamene tikupitiriza ndi chigawo ichi tidzikumbukira kuti amene analankhula mau ali pamwambapa anali Yesu Ndipo pamene ananena 'sungani malamulo anga,' anayamba ndi mau akubetchera, 'ngati mukonda Ine.'

Mkuru mwini chuma anamyankha Yesu mosachedwetsa,"Izi zonse ndazisunga kuyambira ubwana wanga. Ndisowanso chiyani china?" Kumvetsetsa kwake za malamulo kunali kwa kunja kwa thupi komanso kwapamwambapamwamba. M'kaweruzidwe ka umunthu, khalidwe lake linali loyera ndi langwiro. Maonekedwe a moyo wake wakunja kwa thupi anali aja a munthu wolungama wopanda tchimo liri lonse: ndipo mosakayika konse iye amadzimvanso choncho. Koma ngakhale zinali choncho, m'chikumbumtima chake anali ndi mantha kuti chiyanjano mu uzimu pakati pa iye ndi Mulungu sichinali bwino.

Yesu anafunitsitsa kuchiululira ichi kwa mkuru mwini chumayo, ndipo anampatsa phunziro limene linamtsogolera kuti lionekere poyera khalidwe la moyo wake wodzikonda. Iye anadzionetsera kuti amasunga malamulo, koma anasoweka chinthu chimodzi chomwe chinali chofunikira kwambiri cha zonse. Iye analibe chikondi chozama pa Mulungu ndi munthu.

Koma m'yankho lake kwa Yesu, anati, 'Izi zonse ndazisunga kuyambira ubwana wanga.' Werengani Luka 18. Popanda chikondi m'moyo wathu, kungosunga malamulo khumi kokha sichingakhale chiphaso choti tikalowere kumwamba.

Mitima ya anthu ikafewetsedwa ndi kudzazidwa ndi chikoka chakudziletsa cha Mzimu Woyera, iwo amausamala uphungu; koma akatembenuka ndi kukana chidzudzulo kufikira mitima yao italimbitsidwa ngati mwala, Mulungu amalora kuti oterowo atsogoleredwe ndi Satana. Pokana iwo choonadi, amalora chisalungamo, chomwe chimakhala njira ya kuchionongeko chao.

Lonjezano ndi lakuti, "Ngati mukhala mwa Ine, ndi mau anga akhala mwa inu, pemphani chimene chiri chonse muchifuna ndipo chidzachitika kwa inu." Yohane 15:7. Yohane akuchitira ndemanga, "Ndipo umo tizindikira kuti tamzindikira Iye, ngati tisunga malamulo ake. Iye wakunena kuti, Ndimdziwa Iye, koma wosasunga malamulo ake, ali wabodza, ndipo mwa iye mulibe choonadi; koma iye amene akasunga mau ake mwa iyeyu zedi chikondi cha Mulungu chathedwa." 1 Yohane 2:3-5.

"Odala iwo amene atsuka miinjiro yao, kuti akakhale nao ulamuliro pa mtengo wa moyo, ndi kuti akalowe m'mzinda pazipata. Chibvumbulutso 22:14.

Onse amene modzichepetsa ndi pembedzero lonse amafufuza Malembo kuti adziwe ndi kuchita chifuniro cha Mulungu, sangakhale okayikakayika za udindo wao kwa Mulungu. Tiyenera ife kutsatira mau achoonadi chomveka bwino, nthawi iri yonse ya moyo wathu. Kusunga ndi kumvera malamulo kuyenera kudzichitika kuchokera m'chikondi, ndipo kuchita bwino kuyenera kumafunidwa nthawi zonse. Ili ndi khalidwe limene liri lobvomerezeka ndi Mulungu kuloza ku chipulumutso.

Muyeso wa chikhristu choona ukupezeka m'Mau a Mulungu. N'chifukwa chake Yesu anati, "Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga." Yohane 14:15. "Iye wakukhala nao malamulo anga, ndi kuwasunga, iyeyu ndiye wondikonda Ine; koma wondikonda Ine adzakondedwa ndi Atate wanga, ndipo Ine ndidzamkonda, ndipo ndidzadzionetsa ndekha kwa iye. Wosandikonda Ine sasunga mau anga; ndipo mau amene mumva Sali mau anga, koma a Atate wondituma Ine." Yohane 14:21, 23, 24.

## *ALIYENSE ADZALOWA KUMWAMBA: NDI ZOONA?*

Nkhondo yotsutsana ndi malamulo a Mulungu yomwe inayambira Kumwamba, idzapitirira kuchitika mpaka chimariziro cha dziko lapansi. Pamenepo Mulungu adzalionetsera lamulo lake kuti ndi langwiro ndipo adzapulumutsa anthu ake. Satana ndi onse amene ali kumbali yake popandukira Mulungu, adzaonongedwa. Tchimo ndi olichita adzaonongedwa. Anthu okana chifundo cha Mulungu adzakolola chimene akubzala. Mulungu ali chiyambi cha moyo: ndipo munthu akasankha ntchito za uchimo, amadzilekanitsa ndi Iye, ndipo pakutero munthuyo amadzionongа mwini yekha ndi imfa. Iye amayesedwa mlendo "pa moyo wa Mulungu." Khristu akuti, "Onse akundida Ine akonda imfa." Aefeso 4:18; Miy. 8:36. Mulungu amawalora anthu oterowo kukhala ndi moyo kwa kanthawi kuti akonzetsere miyoyo yao kukhala yosinthika. Mbali iri yonse yomwe angasankhe, iwo amalandira mphotho malingana ndi kasankhidwe kao. Posankha moyo wakupandukira, Satana ndi onse omtsatira amadzilekenitsa ndi Mulungu kotero kuti maonekedwe akuwala kwa Mulunguyo kwa iwo amakhala ngati moto wakuwanyeketsa.

Pali makhalidwe omwe munthu ali yense ayenera kuwachita ngati akufuna kulowa m'moyo wosatha. Kumvera ndi kuchita malamulo a Mulungu kumaonetsera za kuyenerezedwa kwa munthu yemwe wafunitsa kulandira unzika wakumwamba pamodzi ndi oyera mtima. Mulungu ali ndi chyang'aniro cha makhalidwe oyenera; ndipo munthu ali yense amene, mwa chisomo cha Khristu, angafikire pa chidzalo cha awa, ali ndi mwayi wonse wolowa mu ufumu wa ulemelero. Ndipo onse amene angafunitsitse kufikira makhalidwe ofunikirawo, ayenera kutsatira zonse zimene Mulungu waziika zotsogolera ku makhalidwe'wo. Ngati munthu akufuna kulowa m'moyo wosatha womwe ndi woyenera ana a Mulungu okha, ayenera iye kukhala wogwira ntchito mnzake ndi Mulungu mokhulupirika. Tinasankhidwa ife kumva zowawa monga Khristu ndi kunyamula gori lake komanso kusenza mtanda wake.

Tiyenera ife kuchita machawi "kukhazikitsa mayitanidwe ndi masankhidwe" athu. 2 Petro 1:10. Tikafufuza m'Malembo, tidzapeza kuti palibe mwana wa Adamu wa mwamuna ndi wamkazi yemwe anasankhidwa ndi kupulumutsidwa ali chikhalire m'kusamvera malamulo a Mulungu.

Bukhu Lopatulika ndi lokhalo maziko a chikhulupiriro ndi chiphunzitso choyenera.

Pali nkhondo yosapeweka patsogolo pa munthu ali yense amene angatsimikizike kugonjetsa machenjerero onse oipa ndi kuchita chipambano. Ntchito yakukonzekera idalira pa munthu ali yense payekha. Sitidzapulumutsidwa m'magulu. Chiyero ndi kudzipereka za munthu wina sizidzakwaniritsa zolephera za munthu wina. Ngakhale pa chiweruzo, mtundu wa anthu udzadutsa m'mapfuko pamaso pa Mulungu, koma chikhalirecho Iye adzaweruza mlandu wa munthu ali yense payekhayekha komanso mosamalitsitsa ngati kuti ndi munthu yekhayo yemwe aweruzidwe ndipo palibe winanso pa dziko lapansi.

Munthu ali yense adzayenera kudzayezedwa ndi kupezedwa wopanda banga kapena khwinya kapena tchimo la mtundu wina uli wonse. Magulu onse awiri amoyo ndi akufa adzaweruzidwa "mwa zolembedwa m'mabuku, monga mwa ntchito zao." Chibvumbulutso 20:12.

Anthu onse adzayenerezedwa mwa chikhulupiriro chao ndi kuweruzidwa monga mwa ntchito zao.

Munthu ali yense asanamizidwe. Malamulo a Mulungu ali chikhalire oyera monga momwe uli mpando wake wachifumu, ndipo ndi malamulo munthu ali yense wokhala m'dziko lapansi adzaweruzidwa. Palibenso muyeso wina umene ntchito za anthu zidzaweruzidwe nao koma malamulo a Mulungu. "Kuchilamulo ndi kuumboni! ngati iwo sanena malinga ndi mau awa. Ndithu mwa iwo mulibe choonadi." Momwe zirirmu, tinene kuti milandu ya anthu idzaweruzidwa pogwiritsa ntchito Mau a Mulungu, kapena pogwiritsa ntchito mabodza obvomerezedwawo a munthu? Khristu akuti, "Mudzawazindikira iwo ndi zipatso zao."

Tipewe ife za chiyero chongodziyenereza cha umunthu chomwe chimabvomereza kumaswa malamulo a Mulungu. Anthu ochita chiyero choterechi sadzayesedwa olungama chifukwa amapondereza malamulo a Mulungu pansi pa mapazi ao, nkumadziweruza ndi muyeso wa chiyero cha eni okha.

Pali gehena yoyenera kuipewa ndi kumwamba kofunika kuti kukhale kwathu.

## *YESU YEKHA AMAPULUMUTSA*

Munthu ndi mkayidi wa Satana ndipo mwachibadwa chake amatsamira ziri zonse zomwe Satanayo amamuuza kuzichita. Mwa iye payekha alibe mphamvu yotha kupewa ndiponso kuligonjetsa tchimo. Ndi pokhapokhapo ngati Khristu angakhale mwa iye mwa chikhulupiriro cha moyo, kulimbikitsa komanso kuwapatsa malingaliro ake mphamvu yochokera kumwamba, kuti munthu angathe kulimbana ndi kumgonjetsa mdaniyo. Chitchinjirizo china chiri chonse chimene iye angachichite payekha sichingamthandize m'njira ina iriyonse. Ndi kudzera mwa Yesu mokha momwe mphamvu ya Satana imagonjetsedwa. Ichitu ndi choonadi chenicheni ndi chofunikira kwambiri kuti munthu ali yense achimvetsetse. Satana ndi wotangwanika nthawi zonse kunka uku ndi uku, kukwera kumwamba ndi kutsika m'dziko lapansi, kufunafuna woti awalikwire. Koma mapemphero a chikhulupiriro cha moyo amagonjetsa mayesero a mphamvu akewo. "Koposa zonse mutadzitengeranso chikopa cha chikhulupiriro chimene mudzakhoza kuzima nacho mibvi yonse yoyaka moto ya woipayo."

Anthu a Mulungu ayenera kumakhala okonzekera kulimbana ndi machenjrero a Satana. Ndi kumkaniza kotero komwe Satanayo amachita nako mantha. Iye amazindikira bwino kuposa ife za malire a mphamvu zake ndi momwe angathe kugonjetsedwera mosabvuta ngati ife titamkaniza moyang'anizana naye mwachindunji. Kudzera mu mphamvu ya umulungu munthu wofookotsetsa mwa oyera mtima amaposa mphamvu zonse za Satana pamodzi ndi za atumiki ake, ndipo ngati woyerayo ali m'mayesero angathe kuonetsera ukuru wake pa ulamuliro wa mdaniyo. Ichi nchifukwa chake Satanayo akamadza kwa munthu amayenda mobisala, ndipo machenjerero ake amakhala akachetechete, ndipo mphamvu zake zimakhala zobisalira ku zinthu zina. Iye samadza modzionetsera poopa kuti angathe kudzutsa chidwi cha kupemphera cha mkhristu yemwe anagona ndi kumpangitsa iye kulumikizana ndi Mulungu m'pemphero.

Kudzera mwa Yesu, chifundo cha Mulungu chinaonekera kwa anthu; koma chifundo sichichotsa chilungamo. Malamulo amaonetsera chenicheni chimene khalidwe la Mulungu liri, ndipo palibe kansonga kapena kalemba kamodzi kangathe kusinthidwa kukwaniritsa chifuniro cha munthu wochimwa. Mulungu sanasinthe malamulo ake, koma anadzipereka nsembe Mwini Yekha, mwa Khristu chifukwa cha chipulumutso cha munthu. "Mulungu anali mwa Khristu alinkuyanjanitsa dziko lapansi kwa Iye yekha." 2 Akor. 5:19.

Malamulo amafuna chilungamo, moyo wa chiyero, khalidwe langwiro; izi palibe munthu angathe kuzipereka. Payekha sangathe kukwaniritsa zofunika za malamulo oyera a Mulungu. Koma Khristu, mwakubwera kwake pa dziko lapansi m'maonekewe a umunthu, anakhala moyo wachiyero, nakula m'machitidwe ndi makhalidwe angwiro. Izi Iye akuzipereka mphatso za ulere kwa onse amene amlandira Iye. Pakutero omlandirawo amakhululukidwa machimo ao akale, kudzera nsoni, chifundo ndi chisomo za Mulungu. Kuonjezera apo, Khristu amawabveka anthu'wo ndi chikhalidwe cha Mulungu. Amalisintha khalidwe la umunthu kulifanizitsa ndi khalidwe la umulungu, m'chikhazikitso choposa cha uzimu wa mphamvu ndi wokoma. Zikatero chilungamo chonse cha malamulo chimapatsidwa mwa wokhulupirira kudzera mwa Khristu. Apatu Mulungu ali, "wolungama, ndi wakumuyesa wolungama iye amene akhulupirira Yesu." Arom. 3:26.

Mwakukhala moyo kwake ndi imfa yake, Khristu anatsimikizira kuti chilungamo cha Mulungu sichinaononge chifundo chake, koma kuti tchimo likhululukidwe, ndiponso kuti lamulo liri chikhalire lolungama ndipo liyenera kumveredwa mwa ngwiro. Apatu bodza la Satana linagonjetsedwa. Mulungu anaonetsera chitsimikizo cha chindunji cha chikondi anachipatsacho kwa munthu.

## UKWATI NDI SABATA ZINAPEREKEDWA M'EDENI

Yesu anatsegulira ntchito yake m'dziko lapansi lino pakudalitsa ubale wa ukwati ku Kana. Iye amene analenga banja loyamba loyera, ndiponso iye amene analenga Paradiso akhalemo makolo athu, anasindikiza chizindikilo chake pa ukwati womwe chisangalalo chake choyamba chinachitikira m'Edeni. Mulungu anamlenga mkazi kuchokera mwa mwamuna, kuti akhale bwenzi ndi womthangatira mwamunayo; akhale m'modzi ndi iye, kumsangalatsa, kumlimbikitsa ndi kumdalitsa iye. Ndipo mwamunayo nayenso akhale m'thandizi wamphamvu wa mkazi wake. Onse omwe amalowa mu ubale wa ukwati m' chiyero, mwamuna kulandira chikondi changwiro kuchokera pansi pa mtima wa mkazi wake, ndi mkazi kupereka chitonthozo pothandizira kukweza khalidwe la mwamuna wake, ndi kumpanga iye kukwanitsidwa, amafitsa cholinga chomwe Mulungu analengera ndikupereka ukwati kwa iwo

Sabata linalengedwa ndi kukhazikitsidwa m'Edeni pachiyambi pa chilengedwe tchimo lisanalowe m'dziko lapansi'li, ndipo Adamu ndi Hava, ndiponso khamu lonse la za kumwamba anali oyambirira kulisunga.

Ukwati monga cholengedwa choyamba, kenaka Sabata zonse zinakhazikitsidwa m'Edeni munthu asanachimwe ndiponso ali wopanda chirema pamaso pa Mulungu. Ziwirizi zinakhazikitsidwa pomwe maziko a dziko lapansi anali nkuyalidwa, muja nyenyezi za m'mawa zinayimba mokondwera, ndi ana a Mulungu anapfuula ndi chimwemwe. Koma anthu anaswa malamulo amene Mulungu anawapatsa ozisungira ndi kuzilemekezera izi, pakutero nadzitengera themberero, kulanga ndi tsoka pa eni okha

## DZIKO LAPANSI NDI POMENYERAPO NKHONDO YA SATANA

Dziko ladzichotsa kwa Mulungu woona. Mipingo ya lero ikulora Satana kulowa ndi kukhala mkati mwao. Mpingo ukanakhalabe m'chiyero ndi m'kuoona mtima, Satana sakanausokeretsa ndi kuutsogolera kukupondereza malamulo a Mulungu. Mu nzeru yake yakuya, Satana akutsutsana mwachindunji ndi maziko a ulamuliro wa Mulungu kuyambira kumwamba ndiponso pa dziko lapansi. Kuukira kwake kunapangitsa kuti iye athamangitsidwe kuchotsedwa kumwamba. Iye amadziwa bwino kuti ngati angawanyenge anthu ena kuswa malamulo osasinthika a Mulungu, amenewo wawatenga kukhala kumbali yake; chifukwa aliyense wakuswa malamulo a Mulungu ayenera kufa imfa yachiwiri. Werengani Chibvumbulutso 20.

Satana anaganizira zopitabe patali ndi nkhondo yake pa malamulo khumi. Iye anauza atumiki ake kuti anthu ena adzachitirabe nsanje nakakamira pa malamulo a Mulungu kotero kuti sadzatheka kugwa m'machenjerero ake; komanso kuti malamulo khumi ndi omveka bwino ndipo anthu ambiri adzakhulupirira kuti akugwirabe ntchito, choncho iye anayenera kupeza njira ina yoliipitsira ndi kutsutsana ndi limodzi la awa. Tsono anawatsogolera atumiki akewo kuyesetsa kusintha lamulo la chinayi, kapena la Sabata, pakutero nasintha lokhalo la khumiwo lomwe ndi chizindikilo cha Mulungu woona, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi. Iye anakutenga kuuka kwa akufa kwa ulemelero kwa Yesu, nawafotokozera iwo kuti popeza kunachitika tsiku loyamba la pa mulungu, ndiye kuti Yesu anasintha la Sabata kuchoka pa tsiku lachisanu ndi chiwiri (Saturday) kukhala pa loyamba la pa mlungu (Sunday).

Pakutero Satana anagwiritsa ntchito kuuka kwa akufa kukwaniritsa cholinga chake. Iye pamodzi ndi atumiki ake anakondwera kwambiri poona kuti bodza lakelo linabvomerezedwa mosabvuta ndi okhulupirira anadzitchawo abwenzi a Khristu. Chimene wina anachikana kuti ndi cholakwika m'chikhristu, wina anachilandira. Umo ndimo ziphunzitso zolakwika zinalandiridwira ndi kutchinjirizidwa ngati zoona. Chifuniro cha chindunji cha Mulungu monga chiri m'mau ake, chinasokonezedwa ndi zolakwika komanso miyambo za umunthu, zomwe zakhala zikuphunzitsidwa ngati kuti ndizo malamulo a Mulungu. Ngakhale ziphunzitso zabodza'zi zidzakhalabe mpaka pakubwera kwachiwiri kwa Yesu, koma mu nthawi yonse yachinyengoyi, Ambuye wakhala ali ndi mboni za choonadi chake. Mkati mwa mdima wa uzimu ndi chizunzo cha mpingo wake pakhala nthawi zonse pali anthu oona mtima ndi okhulupirira omwe anapitiriza kusunga malamulo ake onse mpaka lero.

Ntchito ya Satana ndiyo kukhumudwitsa ndi kuononga, kuchotsa ufulu wa munthu ndi kuononga moyo wake. Kuswa malamulo nthawi zonse kumatsogolera anthu kukhala atumiki a Satana, ndi kuchita zofuna zake zotsutsana ndi Mulungu ndiponso chilungamo chake.

## CHIFUKWA NINJI MKANGANO WA SABATA /SUNDAY?

Satana akuyesetsa kuchotsa chidwi cha anthu kuti asasamalire za Mulungu, komanso kuti asasunge malamulo ake; choncho iye akulimbikitsa makamaka nkhondo yake yolimbana ndi lamulo lokhali lomwe likumuonetsera Mulunguyo kuti ali Mlengi. Iye walimbika mtima kuti chidziwitso cha Mulungu, cha mphamvu yake ya kulenga, zichokeretu m'malingaliro ndi m'chikumbumtima cha anthu. Koma cholinga chakechi sichidzakwanitsidwa chifukwa lamulo'li likusungidwabe, ndikupitiriza kuwalozera anthu kwa Mlengi.

Mtumwi Yuda akuti, "Okondedwa, pakuchita changu chonse chakukulemberani za chipulumutso cha ife tonse, ndafulumidwa mtima ine kukulemberani ndi kudandaulira kuti mulimbanetu chifukwa cha chikhulupiriro chapatsidwa kamodzi kwa oyera mtima." Atumwi ndi ogwira ntchito limodzi nao mu mpingo woyamba amapezana ndi ziphunzitso zosokeretsa zomwe zinadza ndi aphunzitsi onama okhala mu mpingo momwemo. Aphunzitsi onamawo analibe chiphunzitso cha choonadi, ndipo amangonka akuphunzitsa miyambo ndi maganizo a anthu, zimene amagwiritsa malemba apo ndi apo pofuna kuti zioneke ngati choonadi. Kenaka Malemba otengedwa apo ndi apo'wo amayikidwa pamodzi ndikumasandutsidwa ziphunzitso zonama ndi zopanda pake zomwe anthu amene samatha kudziwerengera okha Malembo amazitenga kukhala ngati choonadi cha nthawiyo.

Satana anagwiritsa ntchito aphunzitsi onamawa. Ponamizira kuti anali ndi chikondi pa choonadicho, anabisa cholinga chenicheni, chifukwa uzimu wao unali wakugwa. Ngati iwo akadadza osati m'dzina la Khristu, mosakayika konse akanakanidwa; koma ponamizira kukhulupirira mwa Iye, anakopa chidwi cha okhulupirira ena, ndipo mopanda manyazi ndi kutsutsika m'chikumbumtima chao anachikhotetsa choonadi kukwaniritsa zokhumba za maganizo ao opotoka. Ndipo pamene miyoyo yotayikayi inasiyaniranatu ndi maziko enieni a chikhulupiriro choona, anataya nangula wao, natengekatengeka ngati mchenga wotengekatengeka ndi mafunde a nyanja. Aneneri onama amenewa afotokozedwa m'mau a Mulungu; ndipo ntchito zao zalembedwa m'mabuku akumwamba. Chinyengo ndi zolinga zao, ndiponso ntchito zao zonyansa, sizinazindikirike kwa anthu; koma Ambuye anawerenga zinali m'mitima mwao monga timachitira bukhu lotsegula, ndi kudziwa kuti maganizo ao ndi zolinga zao zinali za chinyengo.

Mtumwi Paulo m'kalata wake wa chiwiri kwa Atesalonika, analosera za chimpanduko chachikuru chomwe chinali nkudza m'tsogolo ndipo chotsatira chake chinali kukhazikitsidwa kwa mphamvu ya upapa. Iye anafotokoza kuti tsiku la Khristu silingafike, " koma chiyambe chifike chipatukocho, nabvumbulutsidwe munthu wosayeruzika, mwana wa chiononongeko, amene atsutsana nazo, nadzikuza pa zonse zotchedwa Mulungu, kapena zopembedzeka; kotero kuti iye wakhala pansi ku Kachisi wa Mulungu, nadzionetsera yekha kuti ali Mulungu." Kupitiriza apo mtumwiyo anachenjezanso antchito anzake kuphatikiza ife, nati, "Pakuti chinsinsi cha kusayeruzika chayambadi kuchita." 2 Atesalonika 2:3, 4, 7. Ngakhale iyi inali nthawi yakumayambiriro enieni a mpingo, koma iye anaona, ziphunzitso zonama, zikulowa mwakachetechete mu mpingo, ziphunzitso zomwe chotsatira chake chinali kukhazikitsidwa kwa upapa.

Pang'ono ndi pang'ono, poyamba monyengelera ndi mwakachetechete, ndipo kenako modzionetsera, chinthu ichi chinanka chikukulirakulira mphamvu ndi kulandiridwa m'maganizo a anthu "chinsinsi cha kusayeruzika" chinapitiriza kupititsa chitsogolo ntchito ya chinyengo ndi yochitira mwano Mulungu. Mosazindikirika ndi wanthu za chenicheni chomwe chinali nkuchitika, miyambo yachikunja inapeza mwayi

wolowera mu mpingo wa Chikhristu. Pa nthawi imeneyi mtima woti nkutsutsa zochitika zonyansazo unali utafoketsedwa ndi chizunzo chimene mpingo unakomana nacho pansi pa ulamuliro wa Romu wa chikunja. Choncho pamene chizunzo chinalekeka, Chikhristu chinalowa m'mabwalo a milandu ndi m'nyumba za mafumu, ndipo unasiya kutsanzira khalidwe lodzichepetsa la Khristu ndi atumwi ake nutsanzira kudzikuza ndi kunyada kwa ansembe ndi mafumu achikunja; ndipo m'malo mwa malamulo a Mulungu unayamba kuphunzitsa maphunzitso ndi miyambo ya anthu. Kutembenuka kwa mfumu Konstantine m'zaka za m'ma 300 A.D. kunasangalatsa Satana kwambiri; ndipo dziko lapansi lobvekedwa maonekedwe a chilungamo, linalowa mu mpingo. Kuchokera pamenepo ntchito yosokoneza ziphunzitso inachitika mothamanga kwambiri. Chikunja chimene chinaoneka ngati chathetsedwa chinakhala chogonjetsa. Machitidwe ake analanamulira mpingo. Ziphunzitso zake, zikondwerero ndiponso zikhulupiriro za zozizwa zinaphatikizidwa m'chikhulupiriro ndi kapembedzedwe ka otsatira a Yesu a nthawiyo.

Kulolerana uku kwa pakati pa chikunja ndi chikhristu kunatsogolera m'kukhazikitsidwa kwa "munthu wakusayeruzika" yemwe analoseredwa kuti adzatsutsana ndi kudzikweza kuposa Mulungu. Mchitidwe waukuru uwu wa chipembedzo uli chipatso cha machenjerero ndi mphamvu ya Satana – chikwaniritso cha kufunitsitsa kwake kukhala pa mpando wa chifumu ndi kulilamulira dziko lapansi chinthu chomwe chakhala chiri cholakalaka cha moyo wake.

Nthawi ina yake Stana anayesera kufuna kupanga mgwirizano ndi Khristu. Anadza kwa Mwana wa Mulungu m'chipululu chamayesero, ndi kumuonetsa Iye maufumu onse a dziko lapansi ndi ulemelero wao, nalonjeza kupatsa awa kwa Iye kukhala ake ngati Iye angamgwadire ndi kubvomereza ulamuliro wa kalonga wa mdimayo. Khristu anamdzudzula woyesa woyerekedwayo namthamangitsa achoke. Koma Satana analichita yesero lomwelo ndi chipambano chachikuru kwa munthu. Pofuna kukhala ndi ulemelero ndi kutchuka za dziko lapansi, mpingo unatsogoleredwa kukufuna kukonderedwa ndi kuthandizidwa ndi anthu otchuka a dziko lapansi; ndi kumkana Khristu.

Anthu ambirimbiri m'Chikhristu akuyenda m'njira monga anayendera Kaini. Mulungu anapereka malamulo ndi malonjezano ake kuti Iye adalitsa onse osunga malamulo ake. Mu lamulo la chinayi iye analamulira anthu kuti adzisunga Sabata, kukhala chikumbutso cha ntchito yake yakulenga komanso ulamuliro wake; koma anthu anafuna kutsatira malamulo ena otsutsana ndi ili, namlora Satana kukhazikitsa pakati pao chikhulupiriro ndi ziphunzitso zomwe ndi za mpingo wongodzitcha wa Chikhristu koma uli wachikunja., kufikira unapondereza ndi kuchotsa Sabata la Ambuye, lomwe ndi chikumbutso cha ntchito ndi mphamvu yake yakulenga, ndi kuliika pambali, pakutero anthu oipa'wo analipanga lamulo'li kukhala lopanda pake, ndipo sabata labodza linayikidwa m'malo mwa loona'lo. Anthu'wo ananama kuti tsiku loyamba la pa mlungu'lo analiika kukhala la sabata chifukwa Khristu anauka kwa akufa pa limenelo ngakhale palibe chitsimikizo chiri chonse chochokera m'mau a Mulungu za kusinthako. "Taonani, kumvera ndiko kokoma koposa nsembe, kutchera khutu koposa mafuta a nkhosa zamphongo." Koma anthu ambiri akunyalanyazabe Malamulo Khumi kotheratu, ndi kumalalikira kuti awa anakhomedwa pa mtanda pamodzi ndi malamulo a zinsembe omwe anali m'thunzi wa nsembe yakudzipereka ya Khristu yomwe inali nkudza. Ponena kuti akupatsa ulemu Mwana wa Mulungu pakusunga tsiku lomwe anauka kwa akufa, iwo akunyoza ndi kupondereza lamulo la Mulungu, ndikuyenda njira monga anachita Kaini yemwe anapereka nsembe zimene Mulungu sanamlamulire, chifukwa chakusamvera malangizo omwe anauzidwa kuwatsatira. Onse amene amamvera Mau a Mulungu monga Abele, amazunzidwa ndi anthu osamvera, ponena za kuzunzidwa ndi kuphedwa monga anachitidwa Abele kuchokera ku dzanja la Kaini, Yohane akuchenjeza, "Musazizwe, abale, likadana nanu dziko lapansi."

Mau a Mulungu ayenera kukhala a ulamuliro waukuru. Ambuye akuti, "Sindidzayipsa chipangano changa, kapena kusintha mau oturuka m'milomo yanga." Mulungu sangasinthe ngakhale kalemba kamodzi ka malamulo ake popanda kusinthika Iye mwini. Anthu sangakhotetse malamulo a Mulungu kukwaniritsa malingaliro ao, ndipo, polephera kugwirizana ndi malamulowo, amawaswa ndi kusokoneza cholinga chao. Mochedwa kwambiri dziko lapansi lidzazindikira kuti silingathe kuwaweruza mau a Mulungu, koma mau a Mulungu ndiwo adzaliweruza dziko. Akadadziwa anthu za kuopsa kwake ndiponso kuipitsitsa kwakulimbana ndi kupikisana ndi Mulungu! Akanadziwa ichi nasiya iwo m'malingaliro ao kutsutsana ndi chifuniro cha Wosaonekayo! Onse amene akutsutsana ndi Mulungu adzaturukira mochedwa kuti pakutero iwo amanyozera ndikudzilekanitsa ndi njira yokhayo yomwe ikadawatsogolera ku chiyero, chimwemwe ndiponso kumwamba.

Mau a Mulungu akufotokoza kuti chilengedwe chinatenga masiku asanu ndi limodzi. Tiyeni tiyerekeze kuti zinamtengera Mulungu tsiku limodzi kapena ngakhale masiku zana limodzi kulenga zonse ndi kumariza. Mosawerengera zakuti zinamtengera Iye masiku angati kuti alenge, tsiku loyamba la pa mulungu liyenera kukhala loyamba la chilengedwe basi. Nkosatheka, kuti tsiku loyambalo, Sunday, likhale la Sabata, lomwe ndi lokumbukiramo za chilengedwe. Tsiku loyamba la pa mlungu'li silinadalitsidwe ndi kupatulidwa ndi pang'ono pomwe.



Mosachita kukayika m'pang'ono ponse anthu adzakhazikitsa malamulo ao otsutsana ndi malamulo a Mulungu. Iwo adzayesetsa kukakamiza malamulo awo'wo m'chikumbumtima cha anthu ena, ndipo ndi changu chonse, adzakakamiza malamulo'wo omwe adzakhala ozunza ndi opondereza okakamizidwawo.

### *CHISINDIKIZO/CHIZINDIKIRO/ CHIZINDIKIRITSO*

Ndi lamulo la chinayi lokha la onse khumi momwe muli chisindikizo cha Iye Wopereka malamulo, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi. Onse amene amasunga lamulo ili amadzibveka ndi dzina {khalidwe] lake, ndipo madalitso onse okhuzana ndi tsiku'li amakhala ao.

Polamulira kusunga ndi kulilemekeza Sabata, inali njira yowalekanitsa ana a Israyeli kuchokera kwa anthu amitundu ina. "Mudzisunga Masabata anga ndithu," anatero Khristu, "pakuti ndiwo chizindikilo pakati pa Ine ndi inu mwa mibadwo yanu;; kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova wakukupatulani." "Ndicho chizindikilo chosatha pakati pa Ine ndi ana a Israyeli; pakuti Yehova analenga zam'mwamba ndi dziko lapansi masiku asanu ndi limodzi, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri, naonanso mphamvu." Chifukwa chake ana a Israyeli azisunga Sabata, kuchita Sabata mwa mibadwo yao, likhale pangano losatha." Eksodo 3i:13, 17, 16.

Sabata liri chizindikiritso cha ubale wapakati pa Mulungu ndi anthu ake, chizindikiritso chakuti iwo ali nzika zake zomvera, ndipo kuti amasunga lamulo lake loyera. Kusunga Sabata kunakhazikitsidwa ndi Mulungu kuti kukhale njira yomzindikirira Iye ndiponso yolekanitsa pakati pa anthu omvera Iye ndi iwo akuswa malamulo ake.

Malamulo a Mulungu ali maziko a kusinthika kosabwerera nako m'mbuyo. Kusunga ndi kuchita malamulo a Mulungu ndi chilimbikitso chopambana pa chiri chonse munthu achichita kuyambira pa ntchito, pa chuma, kuona mtima ndiponso khalidwe la chiyero pakati pa munthu ndi munthu mnzake.

Chikondi chenicheni chimaonetsedwa pakumvera, ndipo chikondi chochitika m'choonadi chimachotsa mantha. Onse amene amakonda Mulungu, amasindikizidwa ndi chizindikilo pa mphumi zao, ndi kuchita ntchito za Mulungu.

Chisindikizo cha Mulungu wamoyo chidzadindidwa pa mphumi pa okhawo amene ali ndi khalidwe lofanana ndi la Khristu. Iwo amene angalilake dziko lapansi, ntchito za thupi ndiponso mdierekezi, ndi okhawo adzasankhidwe kulandira chisindikizo cha Mulungu wamoyocho.

Chisindikizo cha Mulungu sichidzayikidwa pa mphumi ya mwamuna kapena mkazi wosalungama. Sichidzasindikizidwa pa mphumi ya munthu wodzikuza, wokonda za dziko lapansi, kaya woteroyo ndi wamwamuna kapena wamkazi. Sichidzasindikizidwa pa mphumi za amuna kapena akazi a malilime onama kapena a mitima yachinyengo. Onse odzalandira chisindikizo'chi adzakhala okhawo opanda banga la uchimo, - adzakhala iwo oyenera unzika wa kumwamba. Dziwerengereni nokha Malemba, kuti mumvetsetse za kuopsya kwa ora lomwe tirimo.

Iwo amene ali pachiyanjano ndi dziko lapansi, akulandira khalidwe lao loumbika monga mwa dziko lapansi, ndi kukonzetsedwera lemba la chirombo.

Iwo amene achotsa kudzikonda, amene adzichepetsa eni okha pamaso pa Mulungu ndi kuyeretsa mitima yao pakumvera choonadi, awa ndiwo akulandira maumbidwe akumwamba a khalidwe lao, ndipo akukonzekera kulandira chisindikizo cha Mulungu pa mphumi zao. Pamene lamulo likuperekedwa, ndipo chizindikilo cha chirombo chikusindikizidwa, khalidwe lao lidzakhalabe loyera ndi lopanda banga kwa muyaya.

Chizindikiritso, kapena chisindikizo, cha Mulungu, chimaonetsedwa pa kusunga Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri lomwe ndi lokumbukiramo ntchito yakulenga ya Ambuye.

Chizindikilo [chilemba] cha chirombo ndi chosiyana ndi cha Mulungu –ndiko kulilemekeza tsiku loyamba la pa mulungu [Sunday]. "Ndipo [chirombocho] chichita kuti onse, ang'ono, ndi akuru,…alandire chilembo pa dzanja lao lamanja, kapena mkati m'mphumi zao." (Chibv. 13:16). Si pogwiritsa ntchito manja ao kokha pa tsiku la Sunday, komanso osokeretsedwa'wo adzagwiritsa ntchito maganizo ndiponso nzeru zao kulibvomereza ilo kuti ndi

**Ndemanga pa Chibvumbulutso 13:16**

Pamene lamulo lakusunga Sunday lidzakakamizidwa, ndipo anthu adzakhala ataphunzitsidwa bwino za Sabata loona, munthu ali yense amene adzaliswa lamulo la Mulungu ndi kusunga ilo lomwe liribe ulamuliro wochokera kumwamba, koma wa Aroma, adzakhala akulemekeza upapa kuposa Mulungu. Adzapereka ulemu ku Romu, ndiponso ku mphamvu imene idzalimbikitsa sabata lokhazikitsidwa ndi Aroma'li. Pakutero woteroyo adzakhala akupembedza ziwirizo chirombo ndi fano lake.

M'episikopi wa ku Reggio pachifupikitso chake cha zomwe zinakambidwa ku Uphungu wa Trent, anati: "Amipingo ya Mpatuko akumanena kuti akukhulupirira Bukhu Lopatulika lokha basi. Akunena kuti akulitenga Bukhu Lopatulika lokha'lo monga muyeso wa chikhulupiriro chao. Akuukira Mpingo [Katolika] pakunena kuti wapandukira mau a Mulungu ndi kukakamira ku miyambo. Koma zonena za a Mpatukozo kuti maziko a chikhulupiriro chao ndi Bukhu Lopatulika lokha sizoona. Mau ao akuti akhazikika pa Malembo monga muyeso wa chikhulupiriro chao, ndi bodza. UMBONI WA KUNAMAKO: Bukhu Lopatulika mwatchutchutchu likulimbikitsa za kusunga ndi kulilemekeza Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri. Koma a Mpatuko (Protestants) sasunga tsiku lachisanu ndi chiwiri'lo, akulikana. Ngati zikanakhala zoona kuti chikhulupiriro chao chakhazikika pa Malembo okha, akanakhala akusunganso ndi kulilemekeza tsiku lachisanu ndi chiwiri monga zikufunikira m'Bukhu Lopatulika lonse'lo. Komanso iwo sakungokana kusunga tsiku lachisanu ndi chiwiri lomwe ndi la Sabata monga mwa Malembo, koma akusunganso Sunday, lomwe ndi lokhazikitsidwa monga mwa miyambo ya Mpingo [Katolika]. Kuchokera pa mpfundoyi kunena kwao kuti "Bukhu Lopatulika lokha ndilo muyeso wa chikhulupiriro chao" nkunama; ndipo chiphunzitso chophatikiza za 'm'Bukhu Lopatulika ndi miyambo' monga chiriri ndiye kuti ndi chobvomerezeka, ndipo a Mpatuko eni ake ndi mboni." 18th January,1562.

Sipafunikanso kunena mozungulira za nkhani'yi chifukwa m'chitsimikizo cha za chikhulupiriro cha a Mpatuko'cho – cha Chibvomerezo cha ku Augsburg (Agusburg Confession,) 1530, akubvomereza momveka bwino kuti, "kusunga ndi kulilemekeza Tsiku la Ambuye [Sunday]" kunakhazikitsidwa ndi "Mpingo" pawokha.

Munthu wakusayeruzika wachitadi mwa chinsinsi chake cha kusayeruzika kukweza sabata labodza, ndipo opandukira a Mpatuko akuzizwa potsatira Romu ndipo akulitenga lamulo losunga Sabata la Yehova kuti ndi kuukira malamulo a anthu amitundu. Maufumu apanga mgwirizano kulisunga sabata labodza lomwe ndi losabvomerezeka ndi mau ndiponso mabvumbulutso a Mulungu.

Mau a Mulungu akuchenjeza za kuopsya komwe kuli nkudza; talekani choonadi chiturukiridwe ndipo a Mpatuko m'dziko lonse lapansi azindikire chomwe chiri cholinga cha Romu, koma ichi chidzachitika nthawi itatha yakuti nkupewa machenjerero a Satana. Mwakachetechete Romu akukulanso mu mphamvu. Ziphunzitso zake zayambanso kukhala ndi chikoka m'nyumba za malamulo, m'mipingo, ndi m'mitima ya anthu.

Koma chinthu chochititsa chidwi kwambiri ndi chakuti, nkhosa zambiri zokhulupirika za Mulungu ziri m'khola la a Katolika. Mosakayika konse izo zidzamva mau a Mbusa wao akuti, "Turukani m'menemo anthu anga; kuti mungayanjane ndi machimo ake ndi kuti mungalandireko ya miliri yake" Chibvumbulutso 18:4. Palibe munthu aliyense yemwe adzaweruzidwa pokhapokhapo atalandira kuunika ndi kumvetsetsa za kufunikira kwa lamulo lachinayi. "Nthawi za kusadziwako tsono Mulungu analekerera; koma tsopano alinkulamulira anthu onse ponse ponse atembenuke mtima." Machitidwe 17:30.

"...ndi nkhosa zidzamva mau ake; ndipo ayitana nkhosa za iye yekha mayina ao, nazitsogolera kunja. Pamene aturutsa zonse za iye yekha, azitsogolera; ndi nkhosa zimtsata Iye; chifukwa zidziwa mau ake. Koma mlendo sizimtsata, koma zidzamthawa; chifukwa sizidziwa mau a alendo." Yohane 10:3-5.

sabata.

Ngati kuunika kwa choonadi kwakufikirani, ndi kukubvumbulutsirani za Sabata loona la m'lamulo la chinayi ndi kukutsimikizirani kuti palibe pali ponse m'Mau a Mulungu pakubvomereza za kusunga Sunday kukhala lopatulika, koma inu mukukakamirabe kulilemekeza sabata la bodza'li, ndi kukanitsitsa kulisunga ndi kulilemekeza kukhala Sabata loyera lomwe Mulungu ponena za za ilo anati, "tsiku langa lopatulika,"ndiye kuti mwalandira inu chizindikilo/chilemba cha chirombo. Makamaka kulandira chilembaku/chizindikiloku kudzachitika liti? Pamene mudzabvomereza mwa lamulo lomwe lidzakhazikitsidwa ndi munthu kuti musagwire ntchito ya mtundu uli wonse pa Sunday ndi kulitenga tsiku'li kuti ndi lopembedza Mulungu, chikhalirecho mukudziwa kuti palibe umboni uli wonse kuchokera m'Bukhu Lopatulika wakuti Sunday'lo ndi sabata kuchoka pokhala tsiku wamba la ntchito, kutero kudzakhala kulandira chizindikilo cha chirombo, chifukwa munakana chisindikizo cha Mulungu.

Ino ndi nthawi yakukonzekera chifukwa pamene lamulo lidzaperekedwa, pomwepo chizindikiro chidzasindikizidwa.

Sabata lidzakhala choyeserapo chachikuru chakumvera Mulungu; chifukwa liri chomangirira cha choonadi chomwe chikhale chikukanganiridwa mwapadera. Pamene chiyesochi chidzachitika pa anthu, pomwepo kulekana kwa nthawi zonse kudzachitika pakati pa iwo amene ali atumiki enieni a Mulungu ndi iwo osamtumikira Iye. Pamene kusunga ndi kulilemekeza sabata la bodza'li mogwirizana ndi lamulo la dziko, ndi motsutsana ndi lamulo lachinayi kudzakhala kuubvomereza ulamuliro wotsutsana ndi lamulo la Mulungu, kusunga Sabata loona kudzakhala chitsimikizo chakumvera Mlengi. Pamene gulu lina, pobvomereza chizindikiro chakumvera ulamuliro wa dziko lapansi, lidzalandira chilemba/chizindikilo cha chirombo, gulu lina, posankha kumvera ulamuliro wa Mulungu, ndi kuchita chifuniro chake lidzalandira chisindikizo/chizindikilo cha Mulungu.

Ndani angalore kuti adutsidwe ndi mngelo wa Mulungu pamene iye akunka akusindikiza atumiki a Mulungu pa mphumi zao?

Anthu amene akumvera ndi kulilemekeza lamulo lachinayi akusindikizidwa ndi dzina la Mulungu, komanso kulandira madalitso onse omwe amanka ndi kumverako. "Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, Nena ndi Aroni ndi ana ake, ndi kuti, Uzidalitsa ana a Israyeli motero; uziti nao, Yehova akudalitse iwe, nakusunge; Yehova awalitse nkhope yake pa iwe, nakuchitire chisomo; Yehova akweze nkhope yake pa iwe, nakupatse mtendere. Potero ayike dzina langa pa ana a Israyeli; ndipo ndidzawadalitsa." Numeri 6:22-27.

Sabata ndi chizindikilo/chizindikiritso cha Mulungu; liri chisindikizo cha malamulo ake. "Manga umboni, mata chizindikilo pa chilamulo mwa aphunzi anga." "Kuchilamulo ndi kuumboni! Ngati iwo sanena malinga ndi mau awa, ndiye kuti mwa iwo mulibe choonadi." Yesaya 8:16, 20. KJV. Liri chitsimikizo cha ulamuliro ndi mphamvu zake. Liri chizindikiritso chomwe kudzera mwa ichi timamzindikira Iye kuti ali Mulungu, ndipo nkoyenera kuti lifotokozedwe kuti limayikidwa mkati mwa mphumi.

M'mau ena, munthu ali yense amene adzapondereza lamulo la Mulungu'li ndi kusunga/kulilemekeza Sunday lomwe ndi lopangidwa ndi munthu, ameneyo adzalandira chizindikilo/chilembo cha chirombo; chifukwa iye walora kulemekeza ulamuliro wa bodza. Chenjezo lalikuru ndi lochititsa mantha lochokera kumwamba ndi lakuti, "Ngati wina alambira chirombocho, ndi fano lake, nalandira lemba pamphumi pake, kapena pa dzanja lake, iyenso adzamwako ku vinyo wa mkwiyo wa Mulungu, wokonzeka wosasanganiza m'chikho cha mkwiyo wake." Chibvumbulutso 14:9, 10.

Chisindikizo/chidindo chimakhala ndi zinthu zitatu – dzina la munthu – udindo wa munthuyo – malo amene akuchitira ulamuliro wake. Lamulo lachinayi (Sabata) liri ndi zinthu zonse zitatuzi. "Yehova (Dzina), adamariza (Mlengi) zakumwamba ndi dziko lapansi ndi Nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo



(Malo).

Sabata liri chitsimikizo cha ulamuliro wa Mulungu. Ndi chizindikiritso chomwe kudzera mwa icho timamdziwa Mulungu, ichi nchifukwa chake nkoyenera kulifotokoza kuti limayikidwa mkati mwa mphumi. Anthu opembedza ulamuliro, womwe chizindikilo chake ndi Sunday (Chibvumvulutso 13) akufotokozedwa kuti alandira chizindikilo/chilembo cha wolamulira waoyo mkati mwa mphumi zao kapena m'manja mwao.

Pa Ezekieli 9:4 ndi Chibvumbulutso 7:2, 3 chizindikiro /chilembo chikunenedwa kuikidwa mkati mu mphumi za atumiki a Mulungu. Malemba awiri onsewa akunena za nthawi yachionongeko chotsiriza cha anthu osalungama. Chisindikizo/chidindo chizayikidwa/kudindidwa pa anthu a Mulungu monga chowatchinjiriza kuwatetezera iwo kuchionongeko chiri nkudza. Apa liu "pamphumi" likugwiritsidwa ntchito monga chiphiphiritso, kutanthauza nzeru kapena maganizo, monga momwe "mtima" limagwiritsidwanso ntchito kuimira zamkati mwa moyo kapena zokonda. Choncho kuika chizindikilo pamphumi ndi chimodzimodzi kuti " kulemba m'maganizo." Ahebri 10:16.

Nanga anthu amene akusunga malamulo a Mulungu ndi chikhulupiriro cha Yesu ayenera kukhala otani? Ngati angakhale anthu amene akukana kumvera Mulungu posasunga Sabata lake, chisindikizo sichingadindidwe pa iwo. Chisindikizo/chidindo chiri pangano

lochokera kwa Mulungu lotsimikizira za chitchinjirizo changwiro kwa osankhidwa ake (Eksodo 31:13-17). Kusindikizidwa kumatsimikizira kuti munthu ndi wosankhika wa Mulungu. Mulunguyo wampatula munthuyo kukhala wakewake. Ife monga osindikizidwa a Mulungu ndife ogudwa ake a Khristu, ndipo palibe angatichotse m'manja mwake. Ndi chiyani chomwe chimalembedwa mkati mwa mphumi za olungama? Mulungu ndi Yerusalemu Watsopano. "Ndipo ndidzalemba pa iye dzina la Mulungu wanga, ndi dzina la mzinda wa Mulungu wanga." Chibvumbulutso 3:12.

Chisindikizo cha Mulungu wamoyo chidzadindidwa pa iwo okhawo amene ali ndi Khalidwe lofanana ndi la Khristu. Chikondi chimaonetsedwa m'kumvera, ndipo chikondi cha m'choonadi chimachotsa mantha onse. Iwo amene aligonjetsa dziko lapansi, ntchito za thupi ndi mdierekezi adzakhala okondedwa omwe adzalandira chisindikizo cha Mulungu wamoyo.

Kudzali akanzangotsiriza kusindikizidwa anthu a Mulungu mu mphumi zao – palibe chisindikizo kapena chizindikilo chooneka ndi maso chidzaonekera, koma khalidwe lokhazikika m'choonadi mu nzeru ndi mu mzimu ndilo lidzaonekera, kotero kuti sadzatheka kusunthidwa iwo – kudzali atatha kusindikizidwa adzakhala atakonzetsedwa kuima pamaso pa Mulungu Woyera popanda nkhoswe, ndipo nthawi yomweyo Yesu adzalankhula mau otsekera ntchito yake ya kukhala Mkuruwansembe wotitetezera – akadzatsiriza mau'wo, miliri isanu ndi iwiri idzayamba kutsanulidwa.

Nanga inu mukutani mu nthawi yofunikira kwambiri yakukonzekerayi? Iwo amene ali pa mgwirizano ndi dziko lapansi kuumbidwa kwa makhalidwe ao kuli monga mwamachitidwe a dziko ndipo akukonzetsedwa kulandira chizindikilo/chilembo cha chirombo. Ino ndi nthawi yakukonzekera. Tili ndi kumwamba koti kukhale kwathu ndi gehena woti timpewe.

"Iye wakukhala wosalungama achitebe zosalungama; ndi munthu wonyansa akhalebe wonyansa; ndi iye wakukhala wolungama achite cholungama; ndi iye amene ali woyera akhalebe woyeretsedwa." Chibvumbulutso 22:11.

## *TSIKU LACHISANU NDI CHIWIRI LITAIDWA KUNJA*

Kuchita machitidwe achikunja a chipembedzo m'malo mwa machitidwe a chiyero cha mu mtima ndi mkati m'moyo, kukanatengedwabe kukhala chosangalatsa kwa munthu amene ali wosatembenuka monga zinali m'masiku a atumwi. Chifukwa cha ichi, aphunzitsi onyenga akunka akuchurukirachukira, ndipo anthu amazilandira ziphunzitso zao zosokeretsa ndi mitima yao yonse. Ndi cholinga cha Satana kukhotetsa maganizo a anthu chotere kuchokera ku njira yokhayo ya chipulumutso, chikhulupiriro mwa Yesu ndiponso kukusunga malamulo a Mulungu.

Mu m'badwo uli wonse mdani wamkuruyu amadzetsa mayesero molingana ndi momwe zisankho kapena maganizo a anthu aliri. Mu nthawi ya atumwi iye anawatsogolera Ayuda kukweza malamulo a zinsembe ndi kumkana Khristu; mu nthawi yathu ino iye wakuwalimbikitsa anthu ambiri odzitchawo akhristu, omwenso amadzionetsera ngati akulemekeza Khristu koma akunyozera ndi kukana malamulo a Mulungu, ponena iwo kuti malamulo'wo angathe kumaswedwa popanda chobvuta. Ndi udindo wa mtumiki wokhulupirika aliyense wa Mulungu, kuwatsutsa chitsutsire molimbika ndiponso kuwakanitsitsa aphunzitsi opotoza choonadiwa, ndiponso kuchionetsera chinyengo chao poyera kotheratu pogwiritsa ntchito mau achoonadi mopanda mantha.

Mfumu Charles II, pa April 23, 1647 anati, "Ndikudziwa kuti chikondwerero cha kuuka kwa akufa (Easter) chinakhazikitsa ndi ulamuliro womwenso unasintha Sabata la Chiyuda (lomwenso liri Sabata lenileni la Mulungu) kukhala Tsiku la Ambuye kapena Sunday, chifukwa palibe paliponse m'Malembo pomwe panalembedwa kuti Saturday lisamasungidwe, kapena kuti linasinthidwa ndipo Sunday linalamulidwa kusungidwa m'malo mwake. Choncho ndi zomvetsa chisoni kuti ulamuliro wa mpingo unasintha tsiku lina'lo ndi kuika linzake'lo; choncho m'kumvetsetsa kwanga anthu amene akanitsitse kusunga chikondwerero cha kuuka kwa akufa (Easter) kuli bwino abwerere kusunga ndi kulilemekeza Saturday, ndi kulikanitsitsa la Sunday, loyamba la pa mlungu uli wonse." Zotengedwa kuchokera m' Query to the Parliament Commissioners, zolembedwa ndi Mfumu Charles II.

Ambuye anaifotokoza momveka bwino njira yokalowera ku mzinda wa Mulungu; koma wopandukira wamkuruyo wasintha chikwangwani cholozera ku njira ya ku mzindayo ndi kuika chake cha chinyengo, -sabata lonama. Iye akuti, "Ndidzatsutsana ndi cholinga chiri chonse cha Mulungu. Ndidzayipatsa mphamvu nthumwi yanga, munthu wakusayeruzika, kuchotsa chikumbutso cha Mulungu, - la Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri. Pakutero lidzatsimikiza dziko lapansi kuti tsiku limene Mulungu analipatula ndi kulidalitsa lasinthidwa. Tsiku limene'li silidzakumbukikanso m'maganizo a anthu. Ndidzasokoneza za kufunikira kwake. Ndipo m'malo mwake ndidzakhazikitsa tsiku lomwe silinabvomerezedwe ndi Kumwamba, tsiku limene silidzakhala chizindikilo pakati pa Mulungu ndi anthu ake. Ndidzatsogolera anthu amene alilandire tsiku latsopano'lo, kuti alipatse madalitso amene Mulungu anawayika pa tsiku lachisanu ndi chiwiri. Kudzera mwa nthumwi yangayo (munthu wakusayeruzika) ndidzadzikweza mwini ndekha. Tsiku loyamba la pa mlungu'li lidzakwezedwa, ndipo a Mipingo ya Mpatuko pa dziko lonse lapansi adzalilandira sabata lonama'li kuti ndi loona. Kudzera pakusasunga Sabata limene Mulungu analikhazikitsa, ndidzalipepukitsa ndi kunyozetsa malamulo ake onse. Mau akuti, 'Likhale chizindikilo pakati pa ine ndi inu mwa mibadwo yanu yonse,' ndidzawatembenuza kukhala oimira mbali ya sabata langa. Ndikatero dziko lapansi lidzakhala langalanga. Ndidzakhala wolamulira ndiponso kalonga wa dziko lonse. Pakutero ndidzayika maganizo a anthu pansi pa ulamuliro wanga kuti Sabata la Mulungu lipitirirebe kunyozedwa."

Munthu wakusayeruzika wayika sabata la bodza, ndipo akhristu ochurukitsitsa a dziko lapansi alilandira lamulo la upapa'li ndi kukanitsitsa kumvera ndi kulemekeza Mulungu. Apatu Satana akuwatsogolera amuna ndi akazi ku njira yotsutsana ndi yotsogolera ku mzinda wachipulumutso; ndipo ndi unyinji wa anthu omwe akutsatira njira'yi zikutsimikizika kuti si Adamu ndi Hava okha omwe anamvera mau a machenjerero a mdani waupanduyu.

Mdani wa ubwino wa Mulungu watembenuza chikwangwani, kotero kuti chaloza ku njira yakusayeruzika ndi kuipanga iyi ngati njira ya ku chisangalalo. Iye wakana kumpatsa ulemu Mulungu pokana kutsatira chifuniro chake, Pakuti kwalembedwa." Wayesetsa kusintha nthawi ndi chilamulocho. Werengani Daniyeli 7:25..

Panotu pafunika kusamalitsa kwambiri zakuti tsiku liti loyenera kusungidwa monga lakupumula ndi lakupembedza. Ngati Sabata likukanidwa, malamulo nasinthidwa, ndipo tsiku latsopano kapena losiyana ndi la Sabata'lo layikidwa m'malo mwake, malamulo okidwawo sakhalanso a Mulungu chifukwa chisindikizo chake chachotsedwa ndipo liri ndi chisindikizo ndi mphamvu ya ulamuliro wina.

Mu 1519 a Dr Eck, wa ku Romu yemwe anaonetsa ukatswiri potsutsana ndi a Luther ndiponso a Carlstadt analankhula mau akuti, "Pakunena za ulamuliro wa mpingo: Mau a Mulungu akuphunzitsa: kuti, Ukumbukire kusunga Saturday. Masiku asanu ndi limodzi udzigwira ndi kumariza ntchito zako zonse, koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo la Sabata la Ambuye Mulungu wako. Koma, mpingo [wa katolika] mu mphamvu zake wasintha kukuchotsa kusungako pa Saturday ndi kukuika pa Sunday, osati kuchokera m'Malembo, koma mosakayika motsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

**Pakunena za Masiku Opatulika ndi Akusala Kudya:** Sabata likutchulidwa m'ndime zosiyanasiyana m"Malembo, koma palibe pena pali ponse pomwe pakutchulidwapo za kusintha kwa Sabata'lo ndikuikidwa kwa tsiku la Sunday m'malo mwake mu Uthenga Wabwino wa m'Chipangano Chatsopano, kapena m'makalata a Paulo, kapena m'Bukhu lopatulika lonse; choncho kusinthaku kunachitidwa ndi mpingo wa Katolika popanda ulamuliro wa m'Malembo." Dr Eck's Enchiridon (1533).

Pansi pa pangano la chisomo, Mulungu akufuna kumvera kwa ngwiro kuchokera kwa munthu monga anakufuniranso kumvera kotere kuchokera m'Edeni. Munthu wochimwa amene akhulupirira, kudzera mwa Khristu amene anafera mtundu wa anthu, nakhala Dipo la machimo athu, amakhala wosinthika namvera ndi kulemekeza malamulo a Mulungu. Khristu anasunga malamulo m'chiyero, ndipo kudzera mwa Iye munthu aliyense wochimwa sadzaonongedwa, koma adzalandira moyo wosatha. Iye nati, "Ine ndidzipatula ndekha kuti iwonso akhale opatulika m'choonadi." Chifundo chomwe chimaperekedwa kwa munthu chiri mphatso ya kudzipereka nsembe kwa Khristu, "amene anadzipereka yekha m'malo mwa ife, kuti akatiombole ife ku zoipa zonse, nakadziyeretsere yekha anthu akhale ake enieni, achangu pa ntchito zokoma." Kudzera m'ndondomeko ya chipulumutso, Mulungu ali wolungama, komanso wolungamitsa wa munthu yense wokhulupirira mwa Yesu.

Wolemba Masalmo akuti, "Malamulo a Mulungu ali angwiro akubwezera moyo." Mtumwi akufotokoza, "Chotero chilamulo chiri choyera, ndi chilangizo chake nchoyera, ndi cholungama, ndi chabwino."Nanga ndi chifukwa chiyani Ambuye sanasinthe lamulo lake pofuna kuti wochimwa apulumutsidwe, kapena kulora kuti wochimwayo adziliswabe mosasamala? Chifukwa malamulo a Mulunguwo, "achirikizika ku nthawi za nthawi." Mu chiphunzitso chake cha pa phiri Khristu ananena motsindika, "Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri; sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa. Pakuti indetu ndinena kwa inu, Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kake kamodzi sikadzachokera kuchilamulo, kufikira zitachitidwa zonse. Chifukwa chake yense wakumasula limodzi la malangizo amenewa ang'onong'ono, nadzaphunzitsa anthu chomwecho, adzatchulidwa wamng'onong'ono mu Ufumu wa Kumwamba; koma yense wakuchita ndi

| Malamulo Khumi Monga anaperekedwa ndi Mulungu Pa Eksodo 20:2-17 | Malamulo Khumi Monga alembedwera m'Bukhu la Katekisimo wa Mpingo wa Katolika |
|---|---|
| I | I |
| Usakhale ndi milungu ina koma Ine ndekha. | Ine (Ndine) Ambuye Mulungu. Usakhale ndi milungu ina koma Ine ndekha. **(Lamulo lachiwiri'li linachotsedwa ndipo ena otsatirawo anasinthika pakawerengedwe kao)** |
| II | II |
| Usadzipangire iwe wekha fano losema, kapena chifanizo chiri chonse cha zinthu za m'thambo la kumwamba, kapena za m'dziko lapansi, kapena za m'madzi a pansi pa dziko usazipembedzere izo, usazitumikire izo; chifukwa Ine Yehova Mulungu wako ndiri Mulungu wa nsanje, wakulanga ana chif ukwa cha atate ao, kufikira mbadwo wachitatu ndi wachinayi wa iwo amene akudana ndi Ine; ndi kuwachitira chifundo anthu zikwizikwi a iwo amene akondana ndi Ine nasunga malamulo anga. | Usatchule dzina la Ambuye Mulungu wako pachabe. |
| III | III |
| Usatchule dzina la Yehova Mulungu wako pachabe; chifukwa sadzamuyesa iye wosachimwa, amene atchula pachabe dzina lakelo | Uzikumbukira kusunga tsiku la Sabata kukhala lopatulika **(Chisindikizo cha Mulungu chinachotsedwa pa lamulo la Chinayi (4).** |
| IV | IV |
| Uzikumbukira tsiku la Sabata, likhale lopatulika. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumariza ntchito zako zonse; koma tsiku la chisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako; usagwire ntchito iri yonse, kapena iwe wekha, kapena mwana wako wamwamuna, kapena mwana wako wamkazi, kapena wantchito wako wamwamuna, kapena wantchito wako wamkazi, kapena nyama zako, kapena mlendo amene ali m'mudzi mwako; chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamariza zakumwamba ndi za dziko lapansi, ndi nyanja, ndi zonse ziri m'menemo, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chake Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika. | Uzilemekeza atate wako ndi amako. |
| V | V |
| Uzilemekeza atate wako ndi amako; kuti achuruke masiku ako m'dziko limene Yehova Mulungu wako wakupatsa iwe. | Usaphe |
| VI | VI |
| Usaphe | Usachite chigololo |
| VII | VII |
| Usachite chigololo | Usabe |
| VIII | VIII |
| Usabe | Usamnamizire mnzako |
| IX | IX |
| Usamnamizire mnzako | Usasirire mkazi wa mnzako |
| X | X |
| Usasirire nyumba yake ya mnzako, usasirire mkazi wake wa mnzako kapena wa ntchito wake wamwamuna, kapena wantchito wake wamkazi, kapena ng'ombe yake, kapena buru wake, kapena kanthu kali konse ka mnzako. | Usasirire zinthu za m'bale wako. **(Lamulo ili linagawidwa pawiri pofuna kukwanitsa chiwerengero cha Khumi'wo)** |

kuphunzitsa awa, iyeyu adzatchulidwa wamkuru mu Ufumu wa Kumwamba."

Popanda mphamvu ya Mulungu kukhala naye, munthu pa yekha sangachite chipambano chiri chonse tsono mafunso ndi akuti:

**Funso:** Nanga ndi chifukwa chiyani ife timasunga Sunday la munthu m'malo mwa Saturday? **Yankho:** Timasunga Sunday m'malo mwa Saturday chifukwa Mpingo wa Katolika, mu Uphungu wa Laodikaya (A.D. 366) unasintha kupatulika ndi kudalitsidwa kwa Saturday ndi kukuika pa Sunday. *Convert's Catechism of Catholic Doctrine by Rev. Peter Geiermann C.S.S.R. p50 (2nd ed. 1910).*

**Funso:** Mungatsimikizire bwanji kuti Mpingo [Katolika] uli ndi mphamvu yakusintha zikondwerero ndi masiku opatulika? **Yankho:** Pakusintha Sabata kukhala Sunday, chinthu chomwe a Mipingo ya Mpatuko akuchibvomereza; ndipo amadzitsutsa okha, posunga Sunday ndi kumakana kuchita zikondwerero zina zonse zomwe zinakhazikitsidwa ndi Mpingo umodzimodzi womwewo." *An Abridgment of Christian Doctrine (R.C.) Rev. Henry Tuberville D.D. p. 58 (Approved 1833).*

Satana anaphunzitsidwa ndi kudzozedwa m'mabwalo a kumwamba, ndipo ali ndi chidziwitso chakuya cha zabwino ngakhale zoipa. Amatha iye kuphatikiza chinthu chabwino ndi choipa, machitidwe omwe ali mphamvu yake yayikuru yakusokeretsera ana a anthu.

Anthu amene ali ndi mwayi wakuzindikira ndi kuchita chifuniro cha Mulungu, ndi ololedwa kugwira nao ntchito yopatulikayi yofalitsa uthenga ku dziko lonse lapansi. Ndi chofunikira kuti anthu adziwitsidwe kuti adzaweruzidwa molingana ndi muyeso wa chidziwitso chao za Mulungu monga Mlengi. Anthu akakulandira kuunika, ambiri adzasankha mbali yao mwa chidziwitso ndi kuyamba kusunga ndi kulilemekeza Sabata loona. Posachedwapa chizunzo chifukwa cha malamulo okakamiza a Sunday ndi ziphunzitso zina zosokeretsa zidzapangitsa chiphunzitso cha Sabata loona'li kukhala chomveka kwambiri monga zakhala zikuchitikira m'zaka za m'mbuyomu. Pakusunga tsiku lina kapena linzake, anthu adzaonetsera poyera mbali yomwe ali kaya ndi ya Mulungu kapena ya mdani wa Mulungu Wamkurukuru.

Pa Marko 2;27, Yesu anati, Sabata linayikidwa chifukwa cha munthu. Momveka bwino kwambiri, kuposera apo Yesu anafotokoza za umwini wake kuti, Motero Mwana wa munthu ali mwini dzuwa la Sabata lomwe. Choncho mtundu wa anthu ulibe mphamvu iri yonse yakusintha Sabata, tsiku loona la kupembedza kuliika pa tsiku lina la pa mlungu. Kuonjezera pakusintha kwa tsiku lopembedza'lo, nkusinthanso dzina lake politcha ilo "Tsiku la Ambuye," komwe kuli kupitiriza kuonetsa kupandukira Mulungu kwakukuruku, kuiwala kuti, "koma Mau a Mulungu akhala chikhalire." 1 Petro 1:25.

## TSIKU LA AMBUYE

***(Sunday Maziko Enieni a Chipembedzo cha Upapa)***

Clement, mkuru wa sukulu ya ku Alexandria, anabadwa m'chaka cha m'ma A.D. 160 ndi kufa m'ma A.D. 220. M'chaka cha A.D. 194 anali woyamba wa atsogoleri a mpingo (church fathers) kugwiritsa ntchito mau akuti Tsiku la Ambuye m'zolembera zake mu njira yapadera kutanthauza Sunday tsiku loyamba la pa mlungu. Komanso analankhulanso mosiyanitsa kwambiri za Sabata kuti linali tsiku lakupumula, ndi kuti tsiku loyamba la pa mlungu'lo linali la ntchito! Za kusinthidwa kwa Sabata ndi kukhazikitsidwa kwa lotchedwa sabata la Chikhristu'li sananenepo chiri chonse. Za malamulo, khumi iye analemba motere:

"Tiri nao malamulo khumi omwe anapatsidwa kwa Mose, omwe, ndi osabvuta kuwamvetsetsa, ndipo anayikidwa kuzindikiritsa machimo ndi cholinga chotitsogolera ku chipulumutso." *The Instructor, b. iii. Chap. Xii. Testimony of the Fathers by J.N. Andrews.*

Palibe wina ali yense patsogolo pa iye (Clement) yemwe analembapo za Tsiku la Ambuye kutanthauza Sunday. *Truth Triumphant, p. 82.*

Pamene mpingo wa a Aroma unanka ukukulirakulira mphamvu, pomwepo chiphunzitso cha Sunday'nso chinanka chikutchukiratchukira. M'mau ena mipingo yomwe inachokera m'manja mwa atumwi ndi kupitirira m'chiphunzitso cha Khristu ndi cha atumwi inakakamira kotheratu pakusunga tsiku limene Yesu ndi atumwiyo analilemekeza kukhala lopatulika.

Opembedza a anthu a chi- Waldanse omwe anali ozikika kwambiri ndi kutchedwa Anthu a Bukhu Lopatulika, anasunganso Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri la pa mlungu kukhala la mpumulo woyera kwa zaka mazanamazana. Pambuyo pa zaka mazana awiri a Papa Gregory 1 (A.D. 602) atalemba kalata wotsutsana ndi anthu amene anasunga Sabata loona m'zinda wa Romu, uphungu wa mpingo umene unakambirana kwambiri za kufalikira kwa kusunga Sabata unachitika ku Friaul, kumpoto kwa dziko la Italy (C.A.D. 791). Friaul anali chimodzi cha zigawo zazikuru momwe ufumu wa anthu a chi-Lombard unayambira kukhazikitsidwa.



Uphungu'wo, mu ulamuliro wake wakuti akhristu onse adzisunga Tsiku la Ambuye (Sunday), unapitiriza kufotokoza za kusunga Sabata loona komwe kunali kwakukuru ndithu m'mau akuti, "Kuonjezera apo pakunena za Sabata lomwe Ayuda amalisunga, tsiku lotsiriza la pa mlungu, ndi lomwenso anthu wamba pali ponse amalisunga." Pafupifupi pambuyo pa zaka zana limodzi (A.D. 865-867), mkangano wakuru

unabuka pakati pa Mpingo wa Aroma ndi Mpingo wa Ahelene (GreeK) chifukwa cha anthu a chi-Bulgaria amene atangotembenuka kumene anasunga Sabata, monga zikuonetsedwera mu limodzi la mayankho a mafunso zana limodzi ndi asanu ndi limodzi amene a Papa a Nicolas 1 anapereka poyankha zomwe mfumu ya Bulgaria'ko inawamfunsa. *Truth Triumphant, p.170.*

Zolembera za m'munsi'zi zochokera kwa Mason Neale zionetsera kusiyana pa za Sabata pakati pa Mpingo wa Ahelene ndi wa Aroma: "Kusunga ndi kulilemekeza Saturday, ndi chinthu chomwe monga ali yense akudziwira, chadzetsa kusagwirizana kwakukuru pakati pa Ahelene ndi Alatini. *A History of the Holy Eastern Church, General Introduction,* Vol. 1, p. 731.

Pakupitiriza kuchitira umboni za a Waldanse a m'Bohemia, Erasmus akufotokoza kuti mpaka m'zaka za m'ma A.D. 1500 a Bohemia amene'wa sanangolisunga tsiku lachisanu ndi chiwiri'li mokakamira kokha, koma anatchedwanso Eni-Sabata. *Cox, The Literature of the Sabbath Question, vol. 2, pp. 201, 202.*

Kusintha kwa malamulo'ku sikobisikanso lero, kukuchitika poyera m'chiphunzitso cha Mpingo wa Katolika, momwe bukhu la Chikatolika lotchedwa The Catholic Encyclopedia likufotokoza mwatchutchutchu kuti, "Kuonjezera pakusintha tsiku la mpumulo kuchoka pa Sabata la Chiyuda, kapena pa tsiku lachisanu ndi chiwiri la pa mlungu, kukhala pa tsiku loyamba, Mpingo, wasinthanso lamulo la Sabata'lo kukhala lachitatu, komanso kulitcha Sunday Tsiku la Ambuye, ndi kuti ndilo tsiku loyenera kusungidwa loyera." Uphungu wa Trent'wu (Gawo VI, can. Xix) ukudzudzula anthu onse amene akukana kuti Malamulo Khumi akugwirabe ntchito pa akhristu." *Truth Triumphant .36.*

### *"NDIPO IYE… ADZAYESA KUSINTHA NTHAWIZO NDI CHILAMULO" Daniel 7:25*

Panali pa tsiku la Sabata pomwe Ambuye anaonekera kwa mtumwi anaponyedwa pa ndendeyo. Sabata linali loyerabe ndipo linasungidwabe ndi Yohane pa Patmo monga momwe iye anachitira pa nthawi imene ananka akulalikira uthenga m'midzi ndi mizinda ya Yudea. Iye anawalandira kukhala akeake mapangano omwe analonjezedwa kwa iwo akusunga tsiku'li. "Ndinagwidwa ndi Mzimu tsiku la Ambuye," Yohane akufotokoza, "ndipo ndinamva kumbuyo kwanga mau akuru," (ochokera kwa Yesu, Mwana wa munthu ndime 13) ngati a lipenga." Chibvumbulutso 1:10.

"Motero Mwana wa munthu ali mwini dzuwa la Sabata lomwe." M'mau awa muli phunziro lalikuru ndi lolimbikitsa mtima. Chifukwa Sabata linapangidwira munthu , liri tsiku la Ambuye. Ndi la Khristu Mwana wa munthu. Ndipo "Zonse zinalengedwa ndi Iye; ndipo kopanda Iye sikukukanalengedwa kanthu kali konse kolengedwa." Yohane 1:3..

Tsono popeza Iye ndi amene analenga zinthu zonse, analenganso Sabata. Ndipo linapatulidwa ndi Iye kukhala chikumbutso cha chilengedwe. Sabata limamuonetsera Iye monga Mlengi ndi Woyeretsa. Likulalikira kuti Iye amene analenga zinthu zonse za kumwamba ndi za m'dziko lapansi, ndi mwa Yemweyo momwe zinthu zonse zigwirizanika pamodzi, ndipo ali mutu wa mpingo, kotero ndi mphamvu yake ife tiyanjanitsidwanso ndi Mulungu. Ndipo pakunena Iye za a Israyeli, anati, "Ndipo ndinawapatsanso masabata anga akhale chizindikilo pakati pa Ine ndi iwo, kuti adziwe kuti Ine ndine Yehova wakuwapatula." Ezekieli 20:12. Choncho Sabata liri chizindikiritso cha mphamvu ya Khristu yakutipanga ife kukhala oyera. Ndipo likupatsidwa kwa onse amene Khristu awalandira kukhala oyera. Ndipo monga chizindikiritso cha mphamvu yakupatula ndi kuyeretsa, Sabata likupatsidwa kwa onse amene kudzera mwa Iye amakhala mbali ya Israyeli wa Mulungu.

Pamene opembedza a Mulungu adzadziwika chifukwa cha kulisunga ndi kulilemekeza lamulo lachinayi, chifukwa liri chizindikiritso cha mphamvu yake yakulenga, ndiponso umboni wakulamulira kwake kuti munthu adzimpembedza Iye ndi kumpatsa ulemu, - opembedza onama adzadziwika pa machitidwe ao akuswa ndi kuphwanya chikumbutso cha Mlengi'chi, ndi pokweza sabata lokhazikitsidwa ndi Aroma. Chinali chifukwa cha Sunday kuti ulamuliro wa upapa unalankhula modzikweza; ndipo podzitengera pa iwo weni mphamvu ngakhale za dziko, unafuna kugwiritsa ntchito mphamvu'zo kuumiriza anthu kusunga ndi kulilemekeza Sunday kukhala "Tsiku la Ambuye." Koma Bukhu Lopatulika likufotokoza mwatchutchutchu kuti tsiku lachisanu ndi chiwiri, osati loyamba la pa mlungu, ndilo tsiku la Ambuye. Potsimikizira zokhala mwini Sabata, Yesu anati, "Mwana wa munthu ali mwini dzuwa la Sabata lomwe." Lamulo la chinayi likufotokoza kuti, "Koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako." Ndipo kudzera mwa mneneri Yesaya Mulungu akulitcha ili, "Tsiku langa lopatulika" Marko 2:28; Yes. 58:13.

Bodza limene anthu akunka akulilankhula lakuti, Khristu anasintha Sabata likutsutsidwa poyera ndi mau a mwini wake. "Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri: sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa. Pakuti indetu ndinena kwa inu, Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kake kamodzi sikadzachokera kuchilamulo, kufikira zitachitidwa zonse. Chifukwa chake yense wakumasula limodzi la malangizo amenewa ang'onng'ono, nadzaphunzitsa anthu chomwecho, adzatchulidwa wamng'onong'ono mu Ufumu wa Kumwamba; koma yense wakuchita ndi kuphunzitsa awa, iyeyu adzatchulidwa wamkuru mu Ufumu wa Kumwamba." Mateyu 5:17-19.

"Chikhulupiriro chanu chisakhale m'nzeru ya anthu, koma m'mphamvu ya Mulungu." 1 Akorinto 2:5.

"Ndipo palibe mmodzi wa oipa adzazindikira; koma aphunzitsi ndiwo adzazindikira." Danieli 12:10. Mvetsetsani kuti aphunzitsi sakufanizidwa ndi anthu osaphunzira kapena mbuli ayi. Akuyerekezedwa ndi anthu oipa. Nkhani ikunenedwa apa si yanzeru za kusukulu ayi koma khalidwe lokhuzana ndi chiyero.

Ndi chinthu chofunikira ndi chopambana kwambiri kwa munthu ali yense woganiza bwino kuphunzira kuchokera m'Mau a choonadi, kenaka kuyenda m'kuunika ndi kulimbikitsa ena kutsatira chitsanzo chake. Tiyenera kumaliphunzira Bukhu Lopatulika mosamalitsa tsiku ndi tsiku, ndi kumvetsetsa chiphunzitso chiri chonse bwinobwino komanso kumayerekeza lemba ndi lemba linzake. Mothandizidwa ndi mphamvu ya Mulungu tiyenera kumaganizira zinthu mozama mwa ife tokha pozindikira kuti tsiku lina tidzayima ndi kudziyankhira tokha mafunso pamaso pa Mulungu.

### *CHISAUTSO CHACHIKURU NDI CHOTSIRIZA CHA DZIKO LAPANSI*

"Karol Wojtyla (Papa Yohane Paulo II) anasankhidwa kutsogolera bungwe lokhalo la chipembedzo m'dziko lapansi lomwe likugwira ntchito zake pali ponse mwachipambano: ili ndi Mpingo wa pamalo ponse wa Katolika." *Keys of This Blood,* M. Martin (Jesuit, Vatican Insider), tsamb 23.

"Zautengera mchitidwe wa Upapa ndi bungwe lake la Mpingo wa Katolika pafupifupi zaka zokwanira 2000 kuti ufikire pachidzalo chokhala bungwe la chipembedzo lopezeka ponseponse…Wokhala ndi cholinga cha ndale m'machitidwe ake? Inde, wokhala ndi cholinga cha ndale zokhuza dziko lonse lapansi m'machitidwe ake. Chifukwa, kuyang'anitsitsa ndi kulingirira mozama kwambiri, Papa Yohane Paulo II, wodzitchayo Nthumwi ya Khristu, akudzitenga kuti iye ndi woweruza yakhayo wachilungamo wa mgwirizano wa anthu m'mayiko onse okhalamo mtundu wa anthu." *Ibid. masamba 374-375.*

"Kwa zaka mazana khumi ndi asanu kapenanso kuposera apo. Aroma akhala akudziyandikitsa kwambiri ndi anthu wamba ndiponso a m'midzi m'dziko lonse lapansi. *Ibid. tsamba 22.* Chotsatira chake, kumvera malamulo a dziko lake kwa munthu wamba, kudzathetsedwa." *Ibid. tsamba 19.*

"Sikungakhale kulakwitsa, kunena kuti, cholinga chomsankhira Yohane Paulo wachiwiri'yu pa udindo wa Upapa – chinali chakuti utsogoleri wake ukhale mphamvu yomwe iyendetse zikhazikitso zazikuru za upapa zomwe iye anazichitadi pa moyo wake wa tsiku-ndi-tsiku, chaka-ndi-chaka – ndikukhala wopambana mu mpikisanowu, womwe pano wagwira mseu. Chifukwa, chodziwika bwino kwambiri panopa ndi chakuti zonse zimene Yohane Paulo II anazikhazikitsa zokanganira ulamuliro wa dziko lonse zikumphatikiza iye mwini; umunthu wake monga mtsogoleri wa upapa, lingaliro lakalekale lakuti ndi wotsatira pa udindo wa Petro panopa, komanso Mpingo wake wa pamalo ponse monga bungwe la za dziko lapansi ndiponso bungwe la okhulupirira omwe amangika pamodzi mu chiyanjano cha chinsinsi chobvuta kuchimvetsetsa.." *Ibid. tsamba 17.*

Bukhu Lopatulika likufotokoza kuti Aroma adzakhalanso a mphamvu pa dziko ndikuchita nkhondo kulimbana ndi anthu a Mulungu. *Werengani Chibvumbulutso 13.* Iwo adzatsutsana ndi malamulo a Mulungu ndi kuika ao a miyambo m'malo mwake; mchitidwe womwe ndi wa Satana, ndipo pakutero adzasokeretsa dziko lonse lachipembedzo kulilekanitsa ndi Mulungu; monga Mulunguyo wanena, "Pakuti chimene munthu achifesa, chimenenso adzachituta." *Agalatiya 6:7.* "Pakuti mphotho yake ya uchimo [ndi] imfa." *Aroma 6:23.*

Fano la Sunday lidzakhazikitsidwa. Malamulo a umunthu adzakakamiza anthu kulisunga ndi kulilemekeza ili kukhala lopatulika ndi loyera, ndikuliika m'malo mwa Sabata loyera la Mulungu. Anthu adzalankhula mau akuru akuchitira mwano Mulungu, ndi okweza mphamvu ya umunthu wao, ndikudziika pomwe panayenera kukhala Mulungu. Pokhala iwo pansi m'kachisi wa Mulungu adzayesetsa kudzipanga kukhala ngati Mulungu, ndi kudzionetsera iwo eni kuti ali Mulungu.

Kumapeto kwa zonse, maulamuliro onse a dziko lapansi adzagonjetsedwa pansi pa ufumu womwe udzakhazikitsidwa ndi Mulungu wakumwamba, ufumu umene udzakhala wa muyaya. Werengani Chibvumbulutso 11:15. Pamenepo, Mulungu adzapatsa mphotho kwa oyera mtima ndi kuononga ochimwa. Ndipo adzaonetsedwanso kachisi wodzala ndi ulemelero wa Mulungu m'mwamba, ndime 19, ndi likasa, momwe muli Malamulo Khumi. Pakuti malamulo khumi omwe anaperekedwa ku dziko lapansi anali chabe m'thunzi wa a kumwambawo.

Kuonongedwa kwa anthu ochimwa

kudzaphatikiza kuonongedwa kwa uchimo. "Pakuti Mulungu wathu ndiye moto wakunyeketsa." Ahebri 12:29.

Tikuyenera ife kusankha kukhala m'chikondi chachikuru cha Mulungu kapena kutsatira nzeru ya munthu ndikudzamva pachiweruzo chotsiriza Yesu akuti, "Chokani kwa Ine otembereredwa inu, ku moto wa nthawi zonse wokonzedwera mdierekezi ndi amithenga ake." Mateyu 25:41.

### *CHENJEZO LOTSIRIZA*

Kaya taunikidwa za mau a Mulungu kapena ayi koma chilango chachikuru chitigwera. Pamene Yehova alankhula, miyamba imamva, ndipo dziko lapansi limatchera khutu ku Mau ake. Mulungu akuchenjeza anthu ake m'masiku otsiriza, ndi kuwayitanira atsatire "Mwanawankhosa kuli konse amukako." Munthu ali yense wonyozera kuitanirako akunyoza Mulungu ndi Mau ake, ndipo Mulunguyo sadzamsiya woteroyo osamlanga.

Chiphunzitso chakuti Malamulo a Mulungu anathera pa mtanda ndi chimodzi cha machenjerero a Satana chongofuna kuononga nacho mtundu wa anthu.

Pali anthu ena omwe amakhulupirira chiphunzitso chakuti Sabata linalengedwa ndi kupatsidwa kwa Ayuda okha; koma ichi mulibe m'Mau a Mulungu. Iye analipereka Sabata kwa anthu ake a Israyeli kukhala lopatulika lakuti alisamalire; kotero kuti chokhacho chakuti Iye anasankha kukumbutsa ndi kulankhula za malamulo ake kuphatikiza la mpumulo'li m'chipululu cha Sinai, osati m'dziko la Israyeli (Palestine), zikutsimikizira kuti anapereka Sabata'lo kwa anthu amitundu yonse. Chilamulo cha malamulo khumi ndi chakale monga momwe chiri chilengedwe. Choncho nkosatheka kuti Sabata likhale lopatulikira Ayuda okha, koma kuti linalengedwera olengedwa onse. Mulungu anaupereka udindo wosunga ndi kulilemekeza tsiku'li kwa anthu onse. "Sabata," mau akufotokoza momveka bwino, "linayikidwa chifukwa cha munthu." Kwa chifukwa ichi, zimveke bwino kwa onse amene ali m'choopsa chakusokeretsedwa, kuti amvere ndi kusamalitsa chomwe Mau a Mulungu akunena kuposa kumvera zochokera m'maganizo a anthu.

Onse okhala pa dziko posachedwapa adzayima pamaso pa Iye Wopereka malamulo kuyankha mlandu wakuswa malamulo'wo. Alipo anthu ambirimbiri m'mipingo yotchuka omwe sadziwa chiri chonse za tanthauzo lenileni la choonadi cha nthawi ino. Chimariziro chiri pafupi. Ndi angati omwe chifukwa chakusakonzekera za chipulumutso cha miyoyo yao adzalira mowawidwa mtima, "Masika apita, mphakasa yatha, ndipo ife sitinapulutsidwe?"

Kodi ndi liti pomwe anthu amvetsetse kuti Mulungu ndi Mulungu, osati munthu?, ndipo kuti Iye sasintha? Mliri uli wonse, imfa iri yonse, ziri mboni za mphamvu ya uchimo ndiponso za choodadi cha Mulungu wamoyo. Mau a Mulungu ndi moyo, ndipo adzakhala muyaya. Adzakhalitsa ku nthawi za nthawi. Zingatheke bwanji nanga kuti munthu amene akudziwa chomwe Mulungu ali ndi zomwe wachita, kusankha njira ya Satana m'malo mosankha njira ya Mulungu? Pali njira imodzi yokha yofikira ku Paradiso anakanidwayo, ndipo ndi njira yakukhala womvera.

Ndi m'Mau a Mulungu okha mumapezeka chitsogozo cha miyoyo ndi machitidwe oyenera a miyoyo yathu. Mneneri akutsimikizira, "Kuchilamulo ndi kuumboni! Ngati iwo sanena malinga ndi mau awa, ndiye kuti mulibe choonadi mwa iwo." KJV. Martin Luther anapfuula, "Ndi Baibulo, Baibulo lokha, lomwe liri maziko a chikhulupiriro chathu." Ndi udindo wa anthu a Mulungu kulikweza Bukhu Lopatulika kukhala muyeso wa chipembedzo ndiponso maziko a chiyembekezo.

M'episkopi wa Reggio anawatengetsa a Mpatuko (Protestants) powatsutsa za kutsatira kwao miyambo ya chikatolika. Ndi chinthu chanzeru ndi chofunika, kulingirira za zomwe Yesu analankhula motsutsana ndi atsogoleri a mpingo a nthawi yake. "Ndipo inu mupeputsa mau a Mulungu chifukwa cha miyambo yanu. ... Koma andilambira Ine kwachabe, ndikuphunzitsa maphunzitso malangizo a anthu." Mat. 15:6, 9. Yesu Khristu amamva kupweteka kotani akamanyozedwa osasamalidwa! Pamene ulemelero wake ukuphimbidwa ndi khalidwe ndiponso moyo wosayenera wa atumiki ake! Tiyeni alonda oima pa dzipilala za Ziyoni tisamakhale nao pamodzi anthu amene amanyozetsa ndi kuchipanga choonadi chomwe chiri mwa Yesu kukhala chopanda pake. Iwo asachite mgwirizano ndi mabungwe osalemekeza Mulungu, monga upapa, ndi a Mpatuko pokweza miyambo kuposa Mau a Mulungu, nzeru ya umunthu kuposa bvumbulutso, ndiponso mphatso za umunthu kuposa chikoka ndi mphamvu zopambana za umulungu.

Funso lodula kwambiri mu nthawi yathu ino ndi lakuti, "Ndani amene ali kumbali ya Yehova? Ndani adzalumikizana ndi mngelo kulalikira uthenga wa choonadi ku dziko lapansi? Ndani adzakulandira kuunika komwe kudzaliwalira ndi kulidzadza dziko lapansi ndi ulemelero?" Iwo amene adzagwiritsitsa kuwala kumene ali nako, adzalandira kuwala koonjezera. Kuwala koonjezerako kudzawala pa miyoyo imene yadzipereka ku mphamvu yakufewetsa ndi yachisomo chakugonjetsa ya Khristu; ndipo iwo okukonda kuunikako, adzapulumutsidwa ku machenjerero a Satana. Iye (Satana) adzayesetsa ndi mtima wonse kuonetsa, kudzera mu mphamvu yake yakuchita zozizwa, zizindikilo ndi zozizwa zomwe zidzakhala ngati zikuiphimba ntchito ya Mulungu yomwe adzayitsiriza pa dziko lapansi. Anthu onse adzanyengedwa kupatula iwo amene maina ao alembedwa m'bukhu lamoyo la Mwanawankhosa. Pano tikukufunitsitsa kuunika pakunyamula kuli konse kwa phazi lathu kuyenda, chifukwa kuti, tingakodwe m'kusayeruzika kwa ochimwa.

Kukhazikitsidwa kwa bodza m'malo mwa choonadi chidzakhala mchitidwe wotsiriza wa zonse. Pamene bodza lokhazikitsidwa'lo lidzafalikira dziko lonse, Mulungu adzadzionetsera yekha. Pamene malamulo a munthu adzakwezedwa kuposa malamulo a Mulungu, pamene maulamuliro a dziko lapansi'li adzayesetsa kukakamiza anthu kusunga ndi kulemekeza tsiku loyamba la pa mlungu, zindikirani kuti nthawi yakwana kuti Mulungu achitepo kanthu. Iye adzanyamuka mu ulemelero wake ndipo adzaligwedeza dziko mwamphamvu. "pakuti taonani, Yehova adza kuchokera ku malo ake kudzazonda okhala padziko lapansi, chifukwa chakuipa kwao; dziko lidzabvumbulutsa mwazi wake, ndipo silidzabvundikiranso ophedwa ake." Yesaya 26:21.

Pasakhale munthu wogonjera mayesero ndi kuchepetsa kumvera kwake malamulo a Mulungu chifukwa cha kunyoza komwe kudzachitidwa pa malamulo'wo, ndipo ichi ndi chinthu chomwe chitipangitse ife kupemphera ndi mtima ndiponso moyo wathu wonse ndiponso m'mau akuti, "Yafika nyengo yakuti Yehova muchite kanthu; pakuti anaswa chilamulo chanu." Chifukwa chakunyoza kodzachitidwa ndi dziko lonse, sindidzakhala m'modzi wa oukira pa nthawi imene Mulungu adzakhala akufunitsitsa kulemekezedwa ndi kukwezedwa koposa kudzera m'khalidwe langa.

### *CHOONADI CHA MULUNGU SICHIMAKHALA CHOTCHUKA*

Dziko lonse lapansi ndi loipidwa kwambiri ndi anthu amene akulalikira chifuniro cha malamulo a Mulungu, kotero kuti mpingo umene uyesere kuchita chifuniro cha Mulungu'chi ukonzekere kupezana ndi zowawitsa zosaneneka. "Chifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukuru, ndi maulamuliro, ndi akuchita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a choipa m'zakumwamba." Aefeso 6:12.

Nowa anali mlaliki wa chilungamo; koma zolalikira zake zonse zakuchenjeza zinanyozedwa ndi anthu a m'badwo wake omwe anawalalikira. Choonadi sichidzabvomerezedwa ndi dziko lapansi; chifukwa ilo liri pa udani ndi malamulo a Mulungu. Dziko lapansi ndi lodzala ndi uchimo, lodzala ndi bodza, lodzala ndi kusayeruzika. Yesu analalikira choona mokhulupirika, mwachikondi, moona mtima, podzikana mwini yekha; koma dziko lapansi linamlandira? – Ayi; iliponso nthawi imene choonadi chinapezana ndi kuipa mitima kwa anthu komanso kukanidwa kuposa nthawi ya Khristu?

Chodziwika bwino ndi chakuti ngakhale pasapezeke munthu ali yense wosunga Sabata zipumulo zana limodzi kuchokera malo amene inu mukukhala, kondwerani kuti chilengedwe chonse chakumwamba chiri pa chiyanjano ndi inu. Khristu Mpulumutsi wanu ndi angelo akumwamba ali pamodzi nanu. Mukangoitanira pa dzina la Mulungu pa nthawi iri yonse yakusowa kwanu, Iye ndi wokonzeka kukuthandizani. Chitani choonadi m'banja lanu. "Ndinu mboni zanga," anatero Ambuye.

Khristu anati, "Ine ndasunga malamulo a Atate wanga ndipo ndikhala m'chikondi chake." Yesu akutiyesa ife ndi kutiona ngati tingasunge malamulo a Mulungu monga Iye anachitira, ndi kuti ngati titatero, tikhala oyanjana nalo khamu la angelo akumwamba. Mulungu akufuna anthu omvera. Kuukira kunayambira kumwamba; ndipo nkosafunika kuti kudzapezekenso kumeneko. Kodi ife ndife olora kufunafuna njira ya Ambuye, kuchita chilungamo ndi maweruzo ake, kufunafuna chifundo, ndi kuyenda modzichepetsa ndi Mulungu wathu? Ndife olora kulandira lonjezano lakuti, "Yandikirani kwa Mulungu, ndipo adzayandikira kwa inu." Pakuti watimangira ife mzinda, ndipo sachita manyazi kutitchula ife abale ake. Iye adzasonkhanitsa alendo ndi ongogonera kwa Mwini Yekha.

Munthu ali yense amene ali wolora, kwa iye kupatsidwa kuunika kwa choonadi akhala pansi pa pangano ndi udindo woposa monga kunachitidwira kwa mneneri wa Israyeli, yemwe kwa iye, kunananenedwa, "Iwe tsono, wobadwa ndi munthu, ndakuika mlonda wa nyumba ya Israyeli, m'mwemo imva mau a pakamwa panga, nundichenjezere iwo. Ndikati Ine kwa woipa. Woipawe, udzafa ndithu, osanena iwe kumchenjeza woipayo aleke njira yake, woipa uyo adzafa m'mphulupulu yake. Koma mwazi wake ndidzaufuna pa dzanja lako. Koma ukachenjeza woipa za njira yake, aileke; koma iye osaileka njira yake, adzafa m'mphulupulu mwake iye, koma iwe walanditsa moyo wako." Ezek. 33:7-9.

Okhulupirira a choonadi a Khristu samayembekezera kuti choonadi chitchuke ndi kulandiridwa. Potsimikizika iwo pa ntchito yao, amalolera kumva zowawa, pamodzi ndi mtumwi Paulo pozindikira kuti, "chisautso chathu chopepuka cha kanthawi chitichitira ife kulemera koposa kwakukuru ndi kosatha kwa ulemelero." 2 Akor. 4:17.

Tisankhe ife chinthu chabwino chifukwa ndi chabwino basi, ndi kusiya zotsatira zonse kwa Mulungu. Kwa anthu

omvera, achikhulupiriro, ndi opirira, dziko lapansi ndi lodzala ndi makonzedwe a zilakolako zake zambiri. Kudzera mwa anthu oterewo ntchito yakukonzanso kumbali ya uzimu iyenera kuchitika ndi kupita chitsogolo.

Atero Yehova, "Mverani Ine, inu amene mudziwa chilungamo, anthu amene mumtima mwao muli lamulo langa; muasope chitonzo cha anthu, ngakhale kuopsedwa ndi kutukwana kwao. Pakuti njenjete idzawadya ngati chofunda, ndi mbozi zidzawadya ngati ubweya; koma chilungamo changa chidzakhala ku nthawi zonse, ndi chipulumutso changa ku mibadwo yonse." Yesaya 51:7, 8.

### TCHIMO LOSAKHULULUKIDWA LAKUSWA MALAMULO A MULUNGU LIDZAKHALA NDI CHILANGO CHOOPSA ... TISANYOZERE ICHI.

Ndipo pamene Yesu anakhala pa phiri la Azitona, popenyana ndi Kachisi, anamfunsa Iye m'seri Petro, ndi Yakobo ndi Yohane, ndi Andreya, kuti, Tiuzeni, zinthu izi zidzachitika liti? Zokhuza kuonongedwa kwa Yerusalemu ndiponso mathedwe a dziko lapansi. Werengani Marko 13:3-37.

Yesu, poyang'ana za m'badwo wotsiriza, analiona dziko liri m'chinyengo chofanana ndi chimene chinapangitsa kuti Yerusalemu aonongeke. Tchimo lalikuru limene Ayuda analichita linali lokana Khristu; pamene tchimo lalikuru la akhristu a lero ndi lokana malamulo a Mulungu pomwe pakhazikikapo ulamuliro wake kumwamba ndi dziko lapansi. Malamulo a Mulungu akunyozedwa ndi kuchitidwa mwano.

"Pamene Afarisi a kalelo anasunga Sabata loona, Afarisi a lero, popewa chidzudzulo cha lamulo'lo komanso kuoneka kwake ngati lonyozeka, safuna ndi pang'ono pomwe m'moyo wao kulisunga Sabata loona'lo limenenso Ambuye wao analisunga kufikira tsiku la imfa yake, ndiponso atumwi ake analisunganso, potsatira chitsanzo chake, kwa zaka makumi atatu Iye atakwera kumwamba, molingana ndi Malembo Oyera." *Catholic Mirror, Sept. 23, 1893.*

Pofuna kutchuka ndi kubvomerezeka ndi anthu, aphungu adzagonjera ku chikakamizo chofuna lamulo la Sunday. Posunga Sunday'lo lomwe linayikidwa ndi mchitidwe wa Upapa motsutsana ndi lamulo la Mulungu amitundu onse olichita adzadzilekanitsa kotheratu ndi chilungamo cha Mulungu. Monga kuyandikira kwa asilikari ankhondo a chi-Roma chinali chizindikiritso chakuonongedwa komwe kunali pafupi kwa Yerusalemu, ndimo kupandukira Mulungu za Sabataku kukhale chizindikiritso kwa ife kuti kulekelera kwa Mulungu za tchimo'li kwafika pa mapeto. Komanso kukhazikitsidwa kwa lamulo lokakamiza kulemekeza sabata la upapa'li kudzakhalenso chenjezo kwa amoyo okhala pa nthawiyo kuti adzayambe kuthawa kuturuka m'mizinda ikuruikuru msangamsanga.

Mbiri monga yalembedwa m'Bukhu Lopatulika ikhala ikubwerezedwa. Mazunzo adzakhala, mazunzo ochititsa mantha, adzidzidzi adzachitika; ndipo zoopsa izi zidzachitika mofulumizitsa chimodzi pambuyo pa chinzake motsatanatsatana.

Mulungu sadzaononga ochimwa onse, kapena amitundu ya anthu pa nthawi imodzi, koma adzalanga mizinda ndi malo onse momwe anthu adzadzipereka eni okha kutsatira mphamvu ya machenjerero ndi ya atumiki a Satana. Koopsa kwambiri kudzakhala kuonongedwa kwa mizinda ya amitundu, ngakhale Mulungu adzalekererako chifukwa miyoyo ina idzaturuka kuchoka m'chinyengo cha mdaniyo, kulapa ndiponso kutembenuka m'ora lotsiriza monga zinachitikira ku Nineve wakale.

Mosakhulupirira zikwizikwi za mizinda yodzala ndi kusayeruzika, ndiponso uchimo woposera muyeso, idzaonongedwa ndi zibvomezi, moto, ndiponso kusefukira kwa madzi. Dziko lonse lapansi lidzazindikira kuti kuli Mulungu amene adzayionetsera mphamvu ya ulamuliro wake kuti ali Mulungu. Amithenga ake osaoneka ndi maso adzadzetsa chionongeko, chipasuko ndi imfa..

Mipingo yonse m'dziko lathu iyenera kuwachenjeza anthu za machitidwe a Mulungu ndi a amithenga ake pa anthu akale. Mapembedzedwe a miyambo alibe tanthauzo liri lonse. Choonadi chakhala chikuponderezedwa ndi miyambo ndiponso chisalungamo kwa nthawi yayitali. Mulungu akatumiza atumiki ake kwa anthu ochimwa ndi uthenga wakuchenjeza, womwe ochimwa'wo akaumva adziulingirira mwakuya, podziwerengera okha Mabuku ao Opatulika.

Panali kudzipatula, kuturuka kunja kodzilekanitsa ndi anthu osalungama, kuchoka ndiponso kuthawitsa moyo. Umu ndimo zinthu zinachitikira m'nthawi ya Nowa; momwemonso ndi Loti; komanso ndi ophunzira patangotsala pang'ono kuti Yerusalemu aonongedwe; umu ndimo zidzakhaliranso m'masiku otsiriza. Mau a Mulungu akumvekanso m'uthenga wakuchenjeza, ndi kuitana anthu ake kuti adzilekanitse iwo eni kuchoka m'kusayeruzika kwakukuru. Nthawi zowawitsa ziri patsogolo pathu, choncho pali kufunikira kwakukuru kwakuti mabanja aturuke kuchoka m'mizinda , ndi kukakhala m'malo achete momwe angathe kukakhala ndi nthawi ya Mulungu, ndi kuphunzira chifuniro ndi njira zake. M'kanthawi kochepa anthu onse a Mulungu adzakhala ataturuka kuchoka m'mizinda. Zindikirani kuti, palibe mkhristu ndi m'modzi amene anaononongeka nao pakuphwasulidwa kwa Yerusalemu. Khristu anali atawachenjeza omtsatira ake, ndipo onse amene anamvera mau ake anayang'anitsitsa za chizindikiritso chomwe Iye anawapatsa.

Kugwa ndi kupandukira mu chipembedzo kwa dziko lapansi komwe kukuchitika m'masiku otsiriza ano, kunaotsedwa kwa mneneri Yohane m'masomphenya onena za Babulo, "ndiye mudzi waukuru wakuchita ufumu pa mafumu a dziko." Chibvumbulutso 17:18. Mzinda'wu usanaononongeke kuitanira kochokera kumwamba kukuperekedwa, "Turukani m'menenmo, anthu anga; kuti mungayanjane ndi machimo ake,, ndi kuti mungalandireko ya miliri yake." Chibvumbulutso 18:4. Monga m'masiku a Nowa ndi Loti, payenera kukhala kudzipatula kooneka bwino kuchokera ku tchimo ndiponso pakati pa anthu ochimwa. Pasakhale kusakaniza pakati pa za Mulungu ndi za dziko, kapena kubwerera m'mbuyo ku za chuma cha dziko lapansi. "Palibe munthu angathe kukhala kapolo wa Mulungu ndi wa chuma." Mateyu 6:24.

Yesu analilira Yerusalemu, chifukwa cha tchimo ndi kulowerera kwa anthu ake osankhidwa. Pano akuliranso chifukwa cha kulimba mtima kwa iwo amene, podzitcha ogwira ntchito limodzi naye, ndi okwanitsidwa ndi kusachita kanthu. Kodi anthu amene amadziwa za kufunikira kwa kupulumutsa miyoyo akumva kuwawa pamodzi ndi Yesu, za ntchito ndi kulemera komanso chisoni chosakanikira ndi misozi chifukwa cha mizinda yochimwitsitsa ya dziko lapansi? Chionongeko cha mizinda iyi, yomwe pafupifupi kwatunthu iri m'chipembedzo cha mafano, chayandikitsitsa.

Yehova adzaonetsa poyera dziko lomwe likuswa lamulo lake loyera, kuti Iye ndi Mulungu, ndipo kuchoka pa Iye palibenso wina.

### KODI MULUNGU ADZAKHALA NDI ANTHU OYERA?

Mulungu anatilamulira ife, "Muzikhala oyera; pakuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu [ndine] woyera" Levitiko 19:2.

Kukhala woyera ndi kugwirizana ndi Mulungu.

Monga Mulungu ali woyera, Iye akufunanso anthu ake akhale oyera, oona mtima, opanda chidetso; pakuti popanda chiyero palibe m'modzi adzaona Ambuye. (Ahebri 12:14). Onse amene amampembedza Iye m'chiyero ndi m'choonadi adzabvomerezedwa ndi Iye."

Yehova amayeretsa mtima monga momwe ife timaulolera mpweya kulowa m'nyumba zathu. Timatsegula zitseko ndi mazenera, ndi kuponya m'menemo kanthu ka fungo lokoma; timatsegula zitsekozo ndi mazenerawo kwambiri, kuti mpweya wochokera mu mlengalenga ulowemo. Ambuye akuti, "Iye amene achita choonadi, adza kukuunika." Mazenera akupsa mtima, amaganizo a umunthu, ayenera kutsegulidwa kuloza kumwamba, ndipo fumbi la kudzikonda ndi la za dziko liyenera lichotsedwe. Chisomo cha Mulungu chiyenera kusesa mzipinda zonse za maganizo, malingaliro ayenera adzazidwe ndipo zinthu zakumwamba ndizo zidziganizidwa, ndipo mbali iri yonse ya moyo wathu iyenera idziyeretsedwa ndi kulimbikitsidwa ndi Mzimu wa Mulungu.

Satana angathe kumatiuza kuti si chinthu chabwino kusiya tchimo; nkumati tapita patali kwambiri ndi kulakwa kwathu ndiponso kusayeruzika kotero kuti sizingakhale zothandiza kapena za phindu lina liri lonse kwa ife kuyesera kubwereranso kwa Mulungu. Pamene tingathe kumva za kuipitsitsa kwa machimo athu, Yesu yemwe ndi Mkhululukira-tchimo ndi Mpulumutsi amafunitsitsa kulowa m'mitima mwathu.

Ngath ife tingabwere kwa Mulungu monga momwe tiri, popanda chodzitchinjiriza chiri chonse koma kuti Iye anatifera kupulumutsa munthu wochimwitsitsa woposa ochimwa onse, tidzalandira chikhululukiro ngakhale m'ora la khumi ndi chimodzi la mathedwe a mbiri ya dziko lapansi'li. Munthu ayenera kuyanjana ndi Mulungu. Khristu sanafe kupatsa mphamvu yakukugonjetsa kusayeruzika komwe sikunabvomerezedwe ndi kulapidwa. Si machimo onse omwe ayenera kulapidwa pagulu, koma ena ayenera kulapidwa m'seri ndi munthu payekha kwa Mulungu ndiponso kwa anthu amene anawachimwira.

Khristu ndiye ungwiro wa chikhalidwe cha umulungu. Ali chitsanzo chathu choyenera kuchitsatira. Mau A Petro ali ndi tanthauzo lalikuru, "Monga ana omvera osadzifanizitsanso ndi zilakolako zakale pokhala osadziwa inu, komatu monga Iye wakuitana inu ali woyera mtima, khalani inunso oyera mtima m'makhalidwe anu onse; popeza kwalembedwa, Muzikhala oyera mtima, pakuti Ine ndine woyera mtima." 1 Petro 1:14-16.

Mulungu adzayeza onse, ngati momwe anayezera Adamu ndi Hava kuona ngati adzakhala omvera. Kumvera ndi kusamvera kwathu ndiko kudzaonetsera chisankho chathu. Kuyambira kugwa kwa Adamu, anthu mu m'badwo uli wonse akhala akudzitchinjiriza eni okha za machimo ao, nkumati ndi Mulungu amawachimwitsa, pakunena kuti chifukwa nkobvuta kusunga malamulo ake. Ichitu ndi chimodzi cha zimene Satana anachinamizira pa Mulungu kumwamba. Koma kudzikhululukira pakunena, "Nkobvuta kusunga malamulo," chisakhale chinthu chomnamizira Mulungu; chifukwa pamaso pa Iye pamaima Mpulumutsi, zizindikilo za kupakupachikidwa kwake pa mtanda ziri pa thupi lake., monga umboni wakutsimikizira kuti lamulo lingathe

kusungidwa. Sikuti munthu sangathe kusunga lamulo. Koma kuti sakufuna chabe kutero.

Umboni ukuperekedwa kuchokera kwa oyera mtima omwe adzasinthike pa kubwera kwachiwiri kwa Yesu: "Pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse. Chomwecho tonthozanani ndi mau awa." 1 Ates. 4:17, 18.

### NTHAWI YA KUSANKHA MBALI

Mu nthawi yachimariziro cha mbiri ya dziko lapansi ino mau omwe analankhula pa Sinai akulankhulabe, "Usakhale nayo milungu ina koma Ine ndekha." (Eks. 20:3). Munthu mwa chifuniro chake wasankha kutsutsana ndi chifuniro cha Mulungu. Malingaliro a umunthu sangathe kuzemba udindo wao ku mphamvu yomwe iri pamwamba pao. Ziphunzitso-malangizo a anthu zingathe kuchuruka; anthu angathe kuitenga sayansi kukhala mulungu wao ndi chotsutsira nacho mabvumbulutso, ndipo pakutero nkukana malamulo a Mulungu, koma ngakhale zinthu ziri choncho, Mau akulankhulabe mwamphamvu, "Ambuye Mulungu wako udzimgwadira, ndipo Iye yekha yekha udzimlambira." Mat. 4:10.

Iwo amene anamwalira chidziwitso cha malamulo a Mulungu ndi zofuna za lamulo lachinayi chisanaperekedwe sadzayimbidwa mlandu wa tchimo lakuswa Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri. Nzeru ndi chifundo za Mulungu pakupereka kuunika ndi chidziwitso mu nthawi yoyenera, monga anthu analakalakira, ndi yosayerekezeka. Patsogolo pakubwera kwake kudzaweruza dziko lapansi m'chilungamo, Iye ayamba watumiza chenjezo kukweza ndi kukopa chidwi cha anthu kukusiya kunyalanyaza kwao za lamulo lachinayi kuti athe kuunikiridwa, komanso kulapa za kuliswa kwao, ndi kutsimikizika pakudzikhuthula kwatunthu kwa Wopereka lamulo'lo. Iye wapereka mwayi kwa anthu onse omwe angafune kukhala oyera ndi okondwa ngati atasankha kutero. Kuunika kochuruka kwapatsidwa ku m'badwo uno, kuti tiphunzire za chomwe udindo ndi mwayi wathu ziri, ndi kusangalala pakumva choonadi cha mtengo wapatali ndi chosabvuta kuchita nacho ndi cha mphamvu.

"Ngati wina alambira chirombocho, ndi fano lake, nalandira lemba pamphumi pake, kapena pa dzanja lake, iyenso adzamwako ku vinyo wa mkwiyo wa Mulungu, wokonzeka wosasanganiza, m'chikho cha mkwiyo wake; ndipo adzazunzika ndi moto ndi sulfure pamaso pa angelo oyera mtima ndi pamaso pa Mwanawankhosa; ndipo utsi wa kuzunza kwao ukwera ku nthawi za nthawi; ndipo sadzapuma usana ndi usiku iwo akulambira chirombocho ndi fano lake, ndi iye ali yense akalandira lemba la dzina lake." Chibv. 14:9-11.

Malamulo a Mulungu ndi umboni wa Yesu zikutiyeza ife. Ngati tingakhale okhulupirika ndi omvera, Mulungu adzakondwera mwa ife, ndi kutidalitsa monga anthu osankhika a mwini yekha. Ngati chikhulupiriro changwiro ndi chikondi changwiro ndi kumvera zichuruka mwa ife, ndi kugwira ntchito m'mitima yathu monga ali otsatira enieni a Khristu,, tidzakhala ndi chikoka chachikuru. Kuunika kudzaturuka mwa ife, ndi kuingitsa mdima wotizungulira, ndi kukonzetsera ndiponso kukweza onse amene angayandikire pafupi ndi chikoka chochitidwacho, ndi kuitanira ku chidziwitso cha choonadi onse amene afuna kuunikiridwa ndi kuyenda m'njira yakudzichepetsa ndi yakumvera.

Satana atangwanika kukhazikitsa ndondomeko zake zokonzekera chimkangano chotsiriza, pamene anthu onse adzasankhe mbali yao. Tiyeni tichotse mtima wosakhuzidwa-wakusakhala ndi mbali. Nthawi yakuyesedwa kwathu yafika, ndipo ife tiyenera kukhala ndi mbali ya Yesu kapena yotsutsana ndi Iye.

"Chifukwa chake ngati munaukitsidwa pamodzi ndi Khristu, funani za kumwamba, kumene kuli Khristu wokhala pa dzanja lamanja la Mulungu. Lingirirani zakumwamba osati za padziko ayi. Pamene Khristu adzaoneka, ndiye moyo wathu, pamenepo inunso mudzaonekera pamodzi ndi Iye m'ulemelero." Akolose 3:1, 2, 4.

### ZOONJEZERA I

Atsogoleri a mpingo akubvomereza kuti tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi lokhalo la Sabata loona lomwe Mulungu analipatsa ku mtundu wa anthu. Ndikuti ndi Mpingo (wa Katolika) umene unayesetsa kusintha chiyero cha Sabata kuchiika pa Sunday.

Mu lamulo lachinayi Mulungu wakumwamba anapereka langizo la chindunji kwa mtundu wa anthu. Ndipo likupezeka pa Eksodo 2o:8-11.

***M'munsi'mu muli zolembera zingapo zoonjezera zotsimikizira momvetsa chisoni za kuyesetsa kusintha lamulo'li – kuchotsa kupatulika kumene Mulungu anakuika pa tsiku lachisanu ndi chiwiri, ndikukuika m'malo mwake pa tsiku loyamba la pa mlungu kuti limenelo ndilo lopatulika.***

"Ndi kofunikira kuwakumbutsa a Presbyterian , a Baptist, a Methodist, ndi mipingo ya Chikhrstu ina yonse, kuti, Bukhu Lopatulika silikuwabvomereza pena pali ponse za kusunga kwao Sunday. Sunday ndi tsiku la Mpingo wa Katolika." Priest Brady, *M'mau olankhulidwa ku Elizabeth, N.J. March 17, 1903, ndipo analembedwa m'Elizabeth, N.J. News,* March 18, 1903.

"Kuganiza mwakuya ndiponso momwe zinthu zikukhalira, pakungofunika kusankha chimodzi cha ziwirizi; kapena imodzi ya mbali izi: Mpatuko (Protestantism) ndi kusunga Saturday kukhala loyera kapena Chikatolika (Catholicity) ndi kusunga Sunday kukhala loyera. Kulolera kwina kuli konse nkosatheka." – *The Catholic Mirror,* Dec. 23, 1893.

"Kusunga Sunday kwa a Mpatuko ndiko kupereka ulemu, m'malo mwa iwo eni, ku ulamuliro wa Mpingo [Katolika]." – Monsignor Louis Segur, *Playin Talk About the Protestantism of Today, 1868, p. 213.*

"Mpingo wa Katolika … ndi mphamvu ya utumiki wa umulungu, unasintha tsiku kuchokera pa Saturday kukhala pa Sunday." – *Catholic Mirror, Official organ of Cardinal Gibbons,* September 23, 1893.

"A Papa angathe kukonza (kusintha) Lamulo la Mulungu." – Ferraris, *Ecclesiastical Dictionary.*

" Pa dziko lapansi pano talowa ndikukhala m'malo mwa Mulungu wam'mwambamwamba." – Papa Leo XIII, M'kalata yake yolembera ku a Episcopi onse ya pa June 20, 1894., *The Great Encyclical Letters of Leo XIII, p. 304.*

"Ngati a Mpatuko amatsatiradi Bukhu Lopatulika lokha, akanamapembedza Mulungu tsiku la Sabata. Posunga iwo Sunday akusunga lamulo la Mpingo wa Katolika." Albert Smith, Chancellor wa Ardiocese ya Baltimore, kuyankha m'malo mwa a Cardinal m'kalata ya pa February 10, 1920.

"Nditsimikizireni kuchokera m'Bukhu Lopatulika pomwe likunena kuti ndidzilisunga Sunday kukhala loyera. Palibe lamulo lotero m'Bukhu Lopatulika. Ndi lamulo la Mpingo woyera wa Katolika. Bukhu Lopatulika likuti, "Uzikumbukira tsiku la Sabata, likhale lopatulika." Mpingo wa katolika ukuti, Ai. Mu mphamvu za umulungu ndikuthetsa tsiku la Sabata ndikukulamulirani inu kusunga tsiku loyamba la pa mlungu kukhala loyera. Ndipo taonani! Dziko lonse la anthu odzuka likuwerama pansi kumvera lamulo la Mpingo woyera wa Katolika." – Priest Thomas Enright, CSSR, President wa Redeptorist College, Kansas City, Mo., m'phunziro lake ku Hartford, Kansas Weekly Call, February 22, 1884 ndi *The American Sentinel,* a New York Catholic Journal ya June 1893, p. 173.

"Ndi zoona Mpingo wa Katolika ukubvomera kuti kusinthaku unakuchita ndipo chochitikacho chiri CHIZINDIKILO cha mphamvu ya mpingo kwake." – Zochokera mu Ofesi ya a Cardinal Gibbons, kudzera mwa a Chancellor H.F. Thomas, November 11, 1895.

"Sunday ndi chizindikiro cha ulamuliro wathu...Mpingo uli pamwamba pa Bukhu lopatulika, ndipo kusintha kwa kasungidwe ka Sabata ndi chitsimikizo cha izi." *Catholic Record of London, Ontario*, September I, 1923.

"Akhristu ambiri amaganiza kuti Sunday ndi lobvomerezeka ndi Bukhu Lopatulika kukhala lakupembedza. Mpingo wa Katolika ukutsutsa kuti ndiwo unasintha kupembedza kwa chikhristu kuchoka pa Sabata la m'Baibulo (Saturday) kukhala pa Sunday, ndiponso kuti kuyesa kutsutsa za kusinthaku komwe nkosabvomerezeka ndi Bukhu Lopatulika, ndi kusowa chilungamo ndi kukana mphamvu ya Katolika. Ngati a Mpatuko afunitsadi kukhazikitsa ziphunzitso zao m'Bukhu Lopatulika lokha, kulibwino adzipembedzanso pa Saturday." – Rome's Challenge, wwwimmaculateheart.com/maryonline Dec. 2003.

"A mipingo ya Mpatuko m'dziko lapansi lonse, komanso a mpingo wa Adventist anabvomereza,Bukhu Lopatulika kuti ndilo mphunzitsi wao yekhayo wangwiro, koma tsono m'machitidwe ao, kuyambira pamene mipingo yao inakhazikitsidwa m'zaka za m'ma 1500, ndiponso



**(Uthengawu ukufalikira dzko lonse. MOSCOW Pamwambapa)**

pakukhala akuwerenga chitsanzo chimene anthu a mtundu wa Chiyuda anakhala akuchichita kale lonse, iwo akulikana tsiku limene Mulungu analipereka kukhala lompembedza, ndipo motsutsana ndi lamulo la Mulungu'lo, anaganiza zodzisankhira tsiku lina lompembedzera losabvomerezeka kapena kuchitiridwa umboni, m'cholinga chao'cho, wochokera m'zolembera za Bukhu Lopatulika." *Catholic Mirror,* Sept. 2, 1893.

Sabata la M'Bukhu Lopatulika si la Chiyuda. Ndi lake la Mulungu.

Ulosi wa m'Bukhu Lopatulika (Danieli 7:25) ndi mbiri ya dziko (history) zikuchitira umboni zakuti Mpingo wa Katolika ndiwo unasintha Saturday kupita ku Sunday.

Nkosatheka Sunday kukhala mbali ya pangano latsopano chifukwa kusunga kwa Sunday kunayamba pambuyo mwazi wa Yesu utakhetsedwa kale. Mateyu 26:28. Pambuyo pa imfa itachitika, sizimatheka kukhazikitsa pangano. Agalatiya 3:15.

"Ndipo m'mene anadza nao, anawaika pa bwalo la akuru. Ndipo anayankha Petro ndi atumwi, nati, Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu." Machitidwe 5:27, 29.

"Si yense wakunena kwa Ine,

# Chinyengo Chachikuru Chikhala Poyera




Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba; koma wakuchitayo chifuniro cha Atate wanga wa Kumwamba. Ambiri adzati kwa Ine pa tsiku lomwelo, Ambuye, Ambuye, kodi sitinanenera mau m'dzina lanu, ndi m'dzina lanunso kuturutsa mizimu yoipa, ndi kuchita m'dzina lanunso zamphamvu zambiri? Ndipo pamenepo ndidzafukulira iwo, Sindinakudziwani inu nthawi zonse; chokani kwa Ine, inu akuchita kusayeruzika. Mateyu 21-23.

*ZOONJEZERAII*

**"KOMA WOPANDA CHIKHULUPIRIRO SIKUTHEKA KUMKONDWERETSA; PAKUTI IYE WAKUDZA KWA MULUNGU AYENERA KUKHULUPIRIRA KUTI ALIPO, NDI KUTI ALI WOBWEZERA MPHOTHO IWO AKUMFUNA IYE."**

Dziko lapansi latsala pang'ono kuti liweruzidwe. Mulungu wachilungamo ayenera kubwezera chilango za imfa ya Mwana wake. Lero lino anthu akusankha Baraba, ndi kupfuula Mpachikeni Khristu. Adzachitiranso ichi oyera ake. Iwo adzachita ichi monga anachitira ansembe ndi oweruza a Chiyuda pa nthawi imene anamzunza Khristu. Iye, wokhala Mwana wa Mulungu, munthu wosachimwa, anaphedwa chifukwa anawaphunzitsa anthu'wo choonadi chimene sichinawakondweretse kuchimva. Ndipo zoonadi anamteroyo, anali Mwana wa Mulungu wosaoneka.

Anthu amene lero akunyoza chilamulo cha Yehova, osasunga ndi kulemekeza malamulo ake, ali kumbali imodzi ndi wopandukira wamkuruyo. Iwo akunka akulalikira ku dziko lakugwa'li kuti malamulo a Mulungu alibe ntchito. Iwo amene amalalikira ichi kuti ndicho choonadi akusokeretsa anthu, ndipo akupitiriza kuwakhomera malamulo a Mulungu pa mtanda pakati pa mbala ziwiri.

Zoipa zonse zomwe zinachitika m'nthawi ya mtundu wa Chiyuda ndizo zikuchitikanso lero. Mchere wasiya kukolera kwake. Anthu amene lero akuseka ndi kuwunyoza mtundu wa Chiyuda kuti unalephera kuona mwa Khristu kukwaniritsidwa kwa zonse zomwe aneneri analosera, ali mumdima monga anachitira Ayuda'wo. Iwo ngati Ayuda akukhomerabe malamulo a Mulungu pa mtanda, malamulo, amene anapangitsa kuti mphatso ya Mwana wa Mulungu iperekedwe kudziko lapansi. Iwo akupachikabe malamulo a Mulungu, omwe ali maziko a boma lakumwamba ndi a dziko lapansi.

Satana akufunitsitsa kuononga ndi kusokoneza mphamvu ya Malamulo Khumi, powatuma amithenga ake kunka akulalikira kuti Khristu anakhomera malamulo'wa pa mtanda. Mtanda'tu uli chitsutso chamkangano wosatha wochitika chifukwa cha kusasinthika kwa chikhalidwe cha malamulo a Mulungu. Khristu anafa pofunitsitsa kupatsa njira ya chipulumutso kwa anthu ochimwa, ndikufunitsitsa kubwezera chiyero cha lamulo linaswedwa'lo. Malamulo anazokotedwa ndi chala cha Mulungu pa magome a miyala, ndipo Yohane anaona kachisi wa Mulungu wotseguka m'mwamba, ndipo m'kachisimo munali magome a malamulo a chipangano. "Ndinaona, ndipo panatseguka pa Kachisi wa chihema cha umboni m'Mwamba," Chibv. 15:5. Mau a Mulungu adzapitiriza kukhala ndi ulamuliro waukuru kwa muyaya. Yehova atero, "Sindidzayipsa chipangano changa, kapena kusintha mau oturuka m'milomo yanga." Mas. 89:34.

Akhristu ambiri m'dziko lapansi sakuzindikira kuti ndi malamulo a zinsembe okha omwe anasinthidwa pa imfa ya Khristu. Iwo akunka akuphunzitsabe kuti ndi malamulo khumi omwe anakhomedwa pa mtanda. Ndi waukuru mdima wandiweyani umene waphimba nzeru zao. Miyoyo yambiri ya oterewa ili pankhondo yayikuru yolimbana ndi Mulungu. Sangathe kumvera ndi kulemekeza malamulo a Mulunguyo. Ndi pokhapokhapo ngati otere'wa angakhale pa chiyanjano ndi kumvera ndiponso kuwalemekeza malamulo'wa pomwe pakhazikika boma la Mulungu, kuti Khristu angaoneke kukhala wofunikira ndi wa tanthauzo m'moyo wao. Angathe iwo kumadzinamiza kuti Khristu ndi Mpulumutsi wao; koma potsiriza pa zonse Iye azati kwa iwo, Sindikudziwani konse. Simunaonetse ntchito za kutembenuka mtima kotheratu pakusayeruzika kwanu kotsutsana ndi malamulo a Mulungu, choncho nkosatheka inu kukhala ndi chikhulupiriro changwiro mwa Ine, pakuti cholinga changa chinali kudzakwaniritsa ndi kuchikuza chilamulo cha Mulungucho.

Malamulo ozindikiritsa tchimo (khumi) sanakhalepo m'thunzi kapena chiphiphiritso. Analipo munthu asanalengdwe, ndipo adzakhala amuyaya monga mpandowachifumu wa Mulungu uli wamuyaya. Mulungu sanachotsepo kapena kusinthako liri lonse la malamulo ake ndi cholinga chakuti munthu apumulutsidwe; chifukwa malamulo'wo ali maziko a boma lake. Ndi osasinthika, osati nkuwaonjezera kapena kuwachotserapo, ali a uzimu ndi a muyaya. Kuti munthu apulumutsidwe, ndiponso chifukwa cha umuyaya wa malamulowo, kunali kofunikira kuti Mwana wa Mulungu adzipereke yekha nsembe ya kwa machimo. Iye amene sanazindikira tchimo anakhala tchimo m'malo mwathu. Anatifera ife pa Gologotha. Imfa yake ikusonyeza chikondi chodabwitsa cha Mulungu pa munthu, komanso umuyaya wakusasinthika kwa malamulo ake.

Chipulumutso ndicho kusinthika mtima kapena kulengedwanso mwatsopano (2 Akorinto 5:17; Aefeso 2:10). Mphamvu imene inalenga miyamba ndi dziko lapansi, ndi yomweyonso ikuombola, kuyeretsa, ndiponso kupulumutsa. Choncho Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri si chikumbutso cha mphamvu yayikuru yakulenga kokha ya Yesu Khristu, komanso ndi chizindikiritso cha mphamvu ya Khristu yakutipulumutsa ife kuchokera ku tchimo mwa maomboledwe, kapena kulengedwanso mwatsopano. Choncho kusunga ndi kulilemekeza Sabata la tsiku la chisanu ndi chiwiri kuli chibvomerezo cha Khristu kuti ali Mlengi, Mombolo ndi Wotipatula. Sabata liri chikumbutso cha chilengedwe, chizindikiritso cha maomboledwe ndiponso chisindikizo cha kupatulidwa.



Malamulo ndi uthenga wabwino ziri chiyanjano changwiro. Chiri chonse cha ziwirizi chimakweza chinzake. Mwa mpamvu za ukuru wao malamulo amachidzudzula chikumbumtima, ndi kumpanga wochimwa kuona kufunika kwa Khristu za chikhululukiro cha machimo. Uthenga wabwino umayionetsera mphamvu ndi umuyaya wa malamulo. "Ine sindikadazindikira uchimo, koma mwa lamulo ndimo," akutero Paulo. Chizindikiritso cha tchimo, chodziwidwa mwa malamulo, chimamtsogolera wochimwa kwa Mpulumutsi. Naye pakufunitsitsa kupulumutsidwa munthu angadze ndi kudzipereka kwa Iye amene anamfera pa mtanda pa Gologotha. Pakutero angathe kuchitenganso chilungamo cha Khristu; pakuti chimapatsidwa kwa wochimwitsitsa ali yense amene walapa. Atero Mulungu, "Ndipo wakudza kwa Ine sindidzamtaya iye kunja." "Ngati tibvomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chiri chonse." 1 Yohane 1:9.

**Mukafuna kuona, kuwerenga Kapena Kudinda Mabuku:** www.bible-sabbath.com www.earthsfinalwarning.com www.evolution-facts.org www.present-truth.org www.worldincrisis.org www.pathlights.com www.stepstolife.org

MUKAFUNA KUMVA NDI KUDZIWA ZAMBIRI LEMBERANI KU:

**Loud Cry and Family Life Ministries**
P.O. Box 2850,
Blantyre,
Malawi. Central Africa.

**Restoration Seventhday Adventist Ministries**
P. O. Box 510751,
Chipata,
Zambia. Central Africa.

**Advent Prophecy Update**
P.O. Box 70516,
Ndola,
Zambia, Central Africa.